

KUMUITANIRA

YESU POWONEKERA



Tiwerege Mawu a Ambuye. Mu Uthenga wa Mateyu, a—
mutu wa 8, kuyambira ndime ya 23, ife tikuwerenga izi:

*Ndipo pamene iye analowa mu chombo, ophunzira ake
anamatsatira iye.*

*. . . taonani, panauka namondwe wamkulu panyanja,
motero kuti chombocho chinaphimbidwa ndi mafunde:
koma iye anali ali mtulo.*

*Ndipo ophunzira ake anadza kwa iye, ndipo
anamudzutsa iye, kuti, Ambuye, tipulumutseni ife:
ife tikufa.*

*Ndipo iye ananena nawo iwo, Chifukwa chiyani muli
amantha, O inu a chikhulupiriro chochepa? Atatero
iye anauka, ndipo anadzudzula mphepoyo ndi nyanja;
ndipo panali bata lalikulu.*

*Koma munthuyo anazizwa, nanena, Ndi munthu wa
mtundu wanji uyu, kuti ngakhale mphepo ndi nyanja
zikumumvera iye!*

- 2 Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano kwa pemphero.
- 3 Atate athu Akumwamba, ndife okondwa kwambiri usikuuno kudziwa kuti Mmodzi wamkulu uyu Amene amapangitsa mphepo ndi nyanja kuti zimumvere Iye ali ndi ife. Ndife oyamikira kuti tiri nawo umboni waukulu uwu wa moyo Wake mpaka lero, ndi kumadziwa kuti Iye ndi Wamuyaya, ndipo Iye sangakhoze konse kufa. Iye ali wamoyo kwanthawizonse, ndipo wasonyeza chifundo Chake chachikulu kwa ife, ana a anthu mmasiku ano. Ndife anthu osowa, Ambuye, osowa kwambiri mwakuti palibe wina aliyense angakhoze kukwaniritsa zosowa zathu koma Inuyo. Chotero ife tikukuyembekezerani Inu usikuuno kuti mubwere mu kusonkhana kwathu pano, ndi kuti mudzadzidziwitse Nokha kwa ife, potikhululukira machimo athu, kuwonjezera chikhulupiriro chathu, Ambuye, ndi kuchiza matenda athu ndi zotisautsa zathu. Ndipo pamene tidzapita ku nyumba zathu, usikuuno, mulole ife tikakhale okondwa, tikunena monga aja a ku Emau, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu pamene Iye amayankhula nafe m’njira?” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

Inu mukhoza kukhala pansu.

- 4 Ine ndiri ngati Zakeyu; zinthu izi nthawizonse zimakhala zazifupi kwambiri kwa ine. Ine ndikufuna kuti ndiyankhule ndi

inu kwa mphindi pang'ono chabe tsopano ife tisanapempherere odwala. Ndikukuthokozani inu chifukwa cha mgwirizano wanu wabwino, ndi kukhulupirira mu Mzimu, usiku wathawu, pamene ife tinali kuyankhula, ndikudalira kuti kudzakhala kutsanulidwa kwakukulu kwa madalitso Ake.

⁵ Nthawizonse muzikumbukira zomwe ife tadzera pano, ndi kudzayesa kuwonjezera chikhulupiriro chanu mu Kukhalapo Kwake, kuti mukakhoze kulandira icho chimene mwachipempha. Kenako, mwa chikhulupiriro, inu mukhulupirire.

⁶ Tsopano, kumbukirani, mdalitso wachiwombolo uliwonse unagulidwa kale. Mtengo unalipiridwa, ilipo njira imodzi yokha yomwe mudzakhoze kulandirira icho, ndiyo kukhulupirira izo ndi kuvomereza izo. “Iye ndi Wansembe Wamkulu wa chivomerezo chathu.” Ahebri amanena pamenepo, kalata wa Ahebri, amati, “Iye ndi Wansembe Wamkulu wa chivomerezo chathu.” Kuvomereza, ndi kulapa, ndi chinthu chomwe chomwecho, ndithudi. Chotero ife...Iye ndi Wansembe Wamkulu wa chivomerezo chathu, chotero Iye sangakhoze kutichitira ife kalikonse kufikira poyamba titavomereza kuti Iye wachita icho. Ndiyeno pamene ife tivomereza izo, ndiye Iye amakhala Wansembe Wamkulu, mkhalapakati, kuti apite akagwire ntchito pa zimenezo ndi kukazikonza izo. Chotero ife tikupemphera, tikudalira mwa Mulungu usikuuno, mu kukoma mtima Kwake ndi chifundo, kuti Iye atipatsa ife kuchuluka kwa chisomo Chake, usikuuno. Ndipo tsopano, kumbukirani, inu muyenera kuvomereza izo.

⁷ Tsopano tipempherera odwala ife tisanachokepo, kusanjika manja pa iwo, koma ndikukhumba mukanakhala ndi chikhulupiriro chokwanira simuyenera kukhala ndi zimenezo. Ine ndikukhumba inu mukanangomafikira ndi kunena kuti, “Ambuye Yesu, ine ndikukukhulupirirani Inu. Ine—ine...” Iye amakhulupirira Mawu.

⁸ Tsopano, onani, Mulungu ndi wosiyana ndi ife. Ngati—ngati tinganene chinachake kuti inu muchite, ndipo inu nkusakhulupirira icho, chabwino, ife tinganene kuti, “Asiyeni iwo okha. Iwo sakusowa kuti akhulupirire izo.” Koma ameneyo si Mulungu Atate wathu. Iye mosasintha amapanga chinachake kuti akupangitseni inu kuti mukhulupirire. Iye akuyesetsa kuti asunge Mawu Ake, ndipo Iye adzawasunga Mawu Ake.

⁹ Tsopano chifukwa chimene Iye akuchitira zinthu zimene Iye akuchita tsopano, ndi chifukwa chakuti Iye analonjeza kuti adzazichita izo. Osati kuti Iye ayenera kuti achite izo; koma Iye analonjeza kuti adzachita izo, ndipo ndicho chidaliro chathu kuti Iye nthawizonse amasunga lonjezo Lake.

¹⁰ Tsopano aliyense wa inu, pamene inu muli ndi odwala, okondedwa, ndi zina zotero, khalani, ngati iwo sangakhoze...

monga mtsikana wamng'ono apa, iye ndi wamng'ono kwambiri, ndipo iye ali mu chikhalidwe chimenecho chimene iye alimo; basi pamene mukhulupirire, mudzaike manja anu pa mwanayo pamene msonkhano ukupitirira. Ena, omwe ali ndi okonedwa awo, mu mtima mwanu mukamawaganizira iwo; mwa chikhulupiro muwakwezere iwo mmwamba pamaso pa Mulungu, mu pemphero. Tsopano, ndipo, chotero, mukatero mukhulupirire. Pamene chinachake chichitike, inu . . .

¹¹ Inu simungadzipangitse nokha kukhulupirira. Inu, ndi chinachake, ndi khalidwe lomwe liri mwa inu. “Chikhulupiro ndicho chinthu,” osati zolingalira-zongozipanga. “Ndi chitsimikiziro cha zinthu zoyembekezeredwa, umboni wa zinthu zomwe umakhulupirira, ndipo sukuziwona.” Ndipo zonse, zida zonse za Chikhristu tsopano, kumbukirani, zimakhala mwa chikhulupiro. Zauzimu zonse, chikondi, chisangalalo, mtendere, kupirira, ubwino, kufatsa, chipiriro, ndizo zonse zinthu zosawoneka. Ndizo zida zonse za Chikhristu. Mkhristu nthawizonse amayang'ana pa zinthu zomwe sakuziwona, chifukwa iye akuyang'ana pa lonjezo.

¹² Kuno nthawi ina kalelo, zaka zambiri, ndinaitanidwa powonekera, nthawi ina, mchipatala, kuti ndikumapempherere mnyamata yemwe anali akufa, ndi diphtheria yakuda. Ndanenapo izi nthawi zambiri, chifukwa ndi nkhani yosuntha kwambiri kwa ine. Bamboyo anali makamaka bambo wokalamba, ndi amayi. Ndipo mnyamata uyu anali pafupifupi usinkhu wa zaka fortini zakubadwa, ine ndikuganiza, ndipo iye anali mwana wawo yekhayo. Ndipo iye anali akufa, ndi diphtheria yakuda, ndipo chinachake chinachitika kwa mtima wake. Iye anakomoka. Ndipo iwo anali basi. . . Iye basi, oh, basi—anali akuthatha ndi moyo; ine ndayiwala chimene—kugunda kwa mtima wake kunali; kupuma kunali kotsika kwambiri.

¹³ Ndipo bambo wokalambayo amapitirira kumayendera msonkhano, ndi kumapempha, kukamuwona manenjala, ndi aliyense. “Bwerani, mudzapemphere! Bwerani, mudzapemphere! Ndizo zonse, ingobwerani ku chipatala ndi kudzapemphera.”

Amanenjala anati, “Mudzamubweretse iye ku msonkhano.”

¹⁴ Anati “Ife sitingathe kumusuntha iye kuchokera ku chipatala. Iye akufa.” Ndipo anati, “Ngati M'bale Branham atangoti wabwera, kudzamupempha Mulungu, Mulungu adzapereka izo.”

Ine ndinaganiza, “Ndi chikhulupiro bwanji!”

¹⁵ Ine ndinapita ku chipatalako, ndipo madokotala amakana kundilola ine kuti ndilowe. Iwo anati, “Ayi, ndinu bambo wokwatira, muli ndi ana.” Billy Paul anali wamng'ono nthawi

imeneyo. Anati, “Inu simungathe kulowa,” anati, “chifukwa inu muli ndi mwana.”

¹⁶ Ndipo ine ndinati, “Tsopano, ine ndamva kuti dokotalayo ndi Mkatolika.” Ine ndinati, “Ngati wansembe atafuna kuti apereke miyambo yotsiriza kwa mwanayo, ngati iye ali Mkatolika, kodi inu mungamulole iye kuti adzalowemo?”

¹⁷ Anati, “Ndizosiyana. Wansembe alibe ana.” Mukuona? Anati, “Inu mukhoza kumutengera mwana wanu kachilomboko.”

¹⁸ Ndipo ine ndinati, “Koma, taonani, bwana. Mundilole ine nditenge udindowo. Ine ndisaina pepala. Nditenga udindowo. Ngati ine ndiribe chikhulupiriro chokwanira kuti ndipite mmenemo ndiye chifukwa cha izo, ine ndiribe ntchito yolowamo, kuyamba ndi kuyamba.” Kenako ine ndinati, “Koma nditenga udindowo.” Ndipo ndinati, “Taganizani za zimenezo tsopano, ngati mnyamata ameneyo anali Mkatolika, ndipo iye anali akufa; ndipo kodi inu, mwanjira iliyonse, mukanamuletsa wansembe kuti asamupatse iye miyambo yotsiriza ya mpingo?”

Iye anati, “Ayi, sindikanachita zimenezo.”

¹⁹ Ine ndinati, “Ine ndikutanthauza mochuluka basi kwa iwo monga wansembe amachitira kwa Mkatolika.”

²⁰ Ndipo anati, “Chabwino,” ndipo potsiriza iye anavomereza. Anandiveka ine ngati Ku Klux Klan, wa mtundu wina, mtundu wonse uwu wa zinthu pa ine, ndi—ndipo ananditengera ine mmenemo kwa mnyamata wamng’ono uyu, akufa.

²¹ Amake ndi abambo anagwada mbali inayo. Ndipo ine ndinapemphera pemphero laling’ono lophweka, “Ambuye Yesu, ine ndikudalira kuti Inu mumudzutsa mnyamata uyu, pa a- . . . maziko a chikhulupiriro cha abambo ndi amayi,” ndipo ndinaika manja anga pa mwana wamng’ono. Iye anali atakomoka kwa atatu, pafupifupi masiku atatu, ine ndikukhulupirira, ndipo amangopumira movutikira. Ndipo ndinanyamukapo, ndinati, “Ameni.” Ndinapemphera pafupifupi mphindi, ndipo ndinadzukapo.

²² Ndipo bambo wokalambayo anamugwira mayiyo padzanja, ndipo anati, “Tangoganizani za izo, wokonedwa, mnyamata wathu wachira!” Palibepo chisonyezo cha izo nkomwe. Ndipo iwo anali akungokumbatirana wina ndi mzake, ndi kumamuthokoza Ambuye.

²³ Ndipo namwino wamng’ono, mwana wamng’ono, dona wamng’ono, kani, iye mwinamwake anali pafupifupi usinkhu wa zaka eyitini, twente zakubadwa. Iye anali ndi lamba wake wa unamwino, ndipo iye . . . kapena, iye anali namwino womaliza maphunziro. Ndipo iye anati, “Bwana, ine ndikuwopa kuti inu simukumvetsetsa.” Iye anati, “Mnyamatayo akufa.”

Iye anati, “Oh, ayi. Mnyamatayo akhala moyo.” Bamboyo anatero.

²⁴ Ndipo anati, “Inu mungachite bwanji monga chomwecho, ndi zanu...inu mukudziwa kuti mwana wanu akufa, pansu pa kukhutitsidwa kwabodza koteroko konga komwe mwapatsidwa?”

Anati, “Si kukhutitsidwa kwabodza.” Iye...

²⁵ Iye anati, “Taonani.” Tsopano ine ndikhoza...Pakhoza kukhala kuti pali adokotala akhala pano. Ine sindimazidziwa izi zamankhwala, ndi zida za katchulidwe ka zachipatala. Iwo anamupatsa iye mtundu wina wa cardiogram, ndipo mtima wake unali wotsika kwambiri. Unali utatsika kwa nthawi yotalika chomwecho. Adokotala anati...Namwinoyo amabwereza zomwe adokotala, anati iye...“Izo sizinayambe zadziwikapo mu mbiriyakale, ngati mtima utsika chomwecho, kuti iwo ungasitsimuke konse kachiwiri.”

²⁶ Ine sindidzaiwala konse mawonekedwe a bambo wachikulireyo. Munthu wokalamba wowoneka mwa ubamboyo anadzuka ndipo anakaika dzanja lake pa phewa la namwino wamng'onoyo. Iye anati, “Mlongo,” iye anati, “tawona, iwe ukuyang'ana pa choyang'anira chimenecho.” Anati, “Ndizo zonse zimene iwe ukuzidziwa, ndi kuyang'ana pa chimenecho. Koma,” anati, “Ine ndikuyang'ana pa lonjezo Lauzimu.”

²⁷ Mnyamatayo ndi mmishonare ku Africa pakali pano, ali ndi ana atatu. Mukuona? Mukuona? Zimatengera chimene iwe ukuyang'anapo, mwawona. Iye anakhulupirira.

²⁸ Tsopano, ndicho chikhulupiro chomwecho, “Ngati Inu mutabwera ndikudzaika manja Anu pa mwana wanga.” “Ngati Inu mudzayankhule Mawu, wantchito wanga...” Mwaona, ndicho chinachake chimene iwe uli nacho. Inu—inu...

²⁹ Ndiye zimenezo sizinali—sikunali kuchitapo kanthu. Munthu wachikulireyo anakhulupirira zimenezo. Iye anali atagwira Chinachake.

³⁰ Mkazi yemwe anakhudza chovala Chake. “Ngati nditangokhudza chovala Chake!” Ndi zimenezotu. Inu muyenera kuchigwira chikhulupiro chimenecho, pansu mu mtima mwanu. Izo zimakhala ngati kuti inuyo mukunena kuti...

³¹ Inu mukudziwa, iwe mwamuna, ngati ndiwe—ngati ndiwe mwamuna wabwinobwino, palibepo mkazi padziko lapansi amene umamukonda monga mkazi wako. Pakhoza kukhala akazi ena akhoza kukhala owonekako bwino. Pakhoza kukhala akazi amene angakhale—angakhale a—a—akazi okongolerapo, ndi zina zotero. Koma chinachake, ngati umamukonda kwenikweni mkazi wako, pamakhala chinachake mmenemo chimene iwe sumachiwona momwe

iyе amawonekera. Iwe umamukonda iye. Ndipo iwe—iwe sumadziwa chifukwa chake, koma iwe umamukonda iye. Ndipo, akazi, inu chimodzimodzi kwa amuna anu. Inu, inu mumakonda. Ndipo inu atsikana aang'ono kwa abwenzi achinyamata; abwenzi achinyamata kwa bwenzi wa mtsikana. Ngati iwe wakumana naye munthu amene umamudziwa kuti umamukonda, pamakhala chinachake mmenemo chimene umadziwa kuti umawakonda iwo.

³² Chabwino, ndicho chinthu chomwecho chimene chimakhalapo chokhudza chikhulupiriro. Iwe umadziwa kuti zichitika. Sipamakhalapo mthunzi, ziribe kanthu ndi angati anganene motsutsana; iwe umakhulupirabe chinthu chomwecho, chifukwa ndicho chenicheni, chikhulupiriro chenicheni choona. Tsopano mukhale nacho chimenecho usikuuno, pamene ife tikuyankhula pa phunziro ili.

³³ Ine ndayankhula zochuluka kwambiri, ndipo ndakhala ndiri mmisonkhano motalika kwambiri tsopano, ine sindinakhalepo ndi kufooka, nkomwe, kuyambira Khrisimasi. Ndipo ndasasa mawu pang'ono pa mmero panga, chifukwa cha kusintha kwa nyengo, ndi nthawi, ndi zina zotero.

³⁴ Ine ndikufuna ndiyankhule nanu usikuuno pamutu wa, “kumudzutsa Yesu,” kapena: *Kumuitanira Yesu Powonekera*.

³⁵ Kuchokera ku kuwerenga kwathu kwa Lemba, ife tikupeza kuti kunali kukuchitika msonkhano waukulu. Yesu anali akuyendayenda, akuchita zodabwitsa zazikulu, nthawizonse akuchita zabwino, ndiponso kumachita zomwe zinali zokondweretsa kwa Mulungu. Iye nthawizonse ankamukondweretsa Mulungu, koma Iye samadzikondweretsa Yekha, Baibulo linatero. Ndipo ife tikupeza kuti Iye anadzizindikiritisa Yekha bwinobwino, Yemwe Iye anali, mwa ntchito Zake. Ntchito Zake zinkazindikiritisa Yemwe Iye anali.

³⁶ Ndipo ukoma unali utachoka mwa Iye. Iye anakhala akuphunzitsa mafanizo, tsiku lonse, ndipo ukoma unali utachoka mwa Iye. Ndipo Iye anali . . . anali woti akawoloke nyanja, kuwolokera, kupita kutsidya linalo. Pokhala chimene Iye anali, Iye—Iye ankadziwa kuti kunali ntchito yaikulu kutsogoloko, kumbali inayo. Ndipo Iye anatopa kwambiri. Ukoma unali utatuluka mwa Iye, utali wa tsiku lonse, pamene anthu amamukhudza Iye ndi chikhulupiriro chawo, kumukhulupirira Iye, ndi zina zotero. Ndipo Iye anali . . .

³⁷ Ukoma unali utamuchokera Iye, ndipo Iye anali atatopa. Chotero Iye anabwerera kumbuyo kwa ngalawayo ndipo anakagona pa pilo, Lemba limatiuza ife, kuti apume pang'ono pamene ngalawayo inali kuwoloka nyanja, kuwoloka Nyanja ya Galileya, mwayi wopuma pang'ono.

³⁸ Ophunzira Ake anatola nkhami zawo, ndipo anakweza matanga, monga momwe amalinyero amachitira. Iwo, ndicho chimene awo, ambiri a iwo, ntchito yawo. Iwo anali asodzi pamene pa nyanja, ndipo—ndipo iwo ankadziwa momwe angayendetsere ngalawa izi. Ndipo iwo anali atabwerera ku ntchito yawo, akungokhala ndi nthawi yopambana ya chisangalalo, nthawi ya chisangalalo, mwinamwake akuyankhula za zinthu zimene zinali zitachitika tsiku limenelo.

³⁹ Inu mukudziwa, pamakhala chinachake cha izo, kuti pamene ife timuwona Ambuye wathu Yesu akuchita zinthu, ndipo nkukhoza kudziwa kuti ndi Iyeyo, kuti palibe china chingakhoke kuchita zimenezo koma Iye, ife mophweka basi... Pamene tifika pamodzi, ife basi... Aliyense amafuna kuchitira umboni. Aliyense amafuna kunena chinachake, ndipo amafuna kuyankhula za icho. Inu mukhoza kukhala ndi chitsitsimutso ku mpingo wanu; abusa akhoza kuyankhula uthenga wodabwitsa, kapena mlaliki, kapena aliyense yemwe angakhale; kapena mukhoza kuwona chinthu china chikuchitika, kapena chinachake mwa woyandikana nawo, winawake anachiritsidwa. Oyandikana nawo amakumana ndi kukambirana za zimenezo. “Ndi zodabwitsa bwanji! Kodi munalipo? Mukanati muziwone zimenezo. Icho chinali chinthu chopambana kwambiri.” Pamakhala chinachake chokhudza ntchito za Mulungu chimene chimakondoweza mtima wa munthu kuposa china chirichonse chimene chimachitika. Pamakhala... Ndizo basi zochitika zosaiwalika pamene tikumana ndi Ambuye Yesu ndi kuwona zinthu zimene Iye amachita, zazikulu kwambiri ndi zododometsa ndizo njira Zake.

⁴⁰ Tsopano ife tikupeza kuti iwo anali akusangalala pa ntchito zimene zinali zitachitidwa mu chitsitsimutso cha tsiku limenelo, ndipo mwinamwake ine ndikanazifanizitsa ife, usikuuno, mwanjira yomweyo.

⁴¹ Tsopano tangochitira kumene umboni chimodzi cha zitsitsimutso zazikulu, ine ndikukhulupirira, kuti dziko linayamba lachiwonapo, mu zaka teni, zomaliza izi, fifitini. Zakhala ziri—chitsitsimutso, osati monga masiku a Billy Sunday, kapena masiku a chitsitsimutso cha Welsh, kapena masiku a—a chitsitsimutso cha Wesley, kapena chitsitsimutso cha Moody, kapena chitsitsimutso cha Billy Sunday, chakhala chikusesa padziko lonse lapansi, kuzungulira dziko lapansi. Misonkhano yaikulu ya machiritso ndi moto wawukulu wa chitsitsimutso wayaka pafupifupi pa phiri lililonse limene liripo mdziko. Usiku womwe uno, komwe kutali mu maiko aku Afrika, uko mu China ndi Japan, Uthenga uwu ukulalikidwa, ndipo anthu akuchiritsidwa miniti yomwe ino, kuzungulira ndi kuzungulira dziko lapansi. Chakhala chimodzi mwa zitsitsimutso zazikulu, chifukwa, ine ndikukhulupirira, ndi

chimodzi cha zitsitsimutso zotsiriza zomwe dziko lino liti lidzawone, chitsitsimutso chosesa-dziko lapansi.

⁴² Koma tsopano, mzaka zingapo zapitazi, kwakhala chete. Inu simukuwonanso kutengeka mwa anthu, kumene kunkakhalapo.

⁴³ Ine ndikukumbukira za kukhala nawo mwayi, mwa Mzimu Woyera, wotsogolera-chitsitsimutso chimene chinayamba, pamene Mngelo wa Ambuye uja anawonekera pa mtsinje ndipo ananena zimenezo, pafupifupi zaka zambiri zapitazo. Ndipo kuziwona izo zikuchitika, ndi kuziwona izo zikuyatsa mitima ya atumiki, konsekonse, zitsitsimutso zinafalikira. Bwanji, iwe umakhoza kungoyenda mophweka kulowa mnyumba, ndipo anthu amangonyamuka kuchoka pa nsalu zawo ndi machira, ndipo nkuchokapo, atachiritsidwa. Iwe sumasowa ngakhale kuti unene mawu amodzi. Basi—basi kungokhala pamene, ndizo zonse zomwe zimatengera.

⁴⁴ Ndikukumbukira usiku wina ku Vandalia, Illinois. Ine ndinalowa mu msonkhano, ndipo ndinali ndisanakhalenso mu msonkhano kwa mphindi faivi, ndipo panalibe munthu wofooka pamalopo, paliponsepo. Zikuku zikukankhidwira kunja ndi kumakawunjikidwa. Akhungu amawona, ndi ogontha ndi osayankhula kumayankhula, ndipo—ndipo mophweka basi... Mzimu wa Ambuye umakhalapo, ndipo Iye amangochiritsa gulu lonselo la iwo. Tsopano ndi pamene iwe ukhoza kuchita chinachake, pamene chitsitsimutso chikuchitika. Koma mulole moto wa chitsitsimutso umenewo ufe, ndiye iwe sungakhoze nkomwe... Anthu akadali Akhristu, koma iwo sanatsitsimutsidwe kulowa mu Mzimu umenewo, chikhalidwe chachikulu chimenecho chimene chimachita chinachake.

⁴⁵ Zimakhala ngati mu chipala, mu sitolo yosula zitsulo. Iwe umayenera kuchitenthetsa chitsulo usanapite kukachimenya icho posulira. Ngati sutero, iwe sudzachiwongola konse icho.

⁴⁶ Ndipo ndi chimene chimatengera kuti ukhale ndi chitsitsimutso, aliylene akhale pansa pa kutentha kwa Mzimu Woyera yemwe watsitsira pansa mphamvu za Mulungu ndi chitsitsimutso kumasuntha. Zikatero pamakhala misonkhano ya mapemphero ikuchitika, usana ndi usiku, miniti iliyonse, konsekonse. Bwanji, anthu sangachoke nkomwe pabwalopo!

⁴⁷ Ine ndikukumbukira mu Jonesboro, Arkansas, pamene ndinayamba koyamba wanga... pafupifupi msonkhano wanga wachitatu. Woyamba mu St. Louis, ndipo kenako ku Corning, ndiyeno kumusi ku Jonesboro. Pepalalo linati, "Anthu twente-eyiti sauzande mu msonkhano." Kwa mailosi twente kapena sarte kuchokera mu mzindawo, anangokhala mahema atakhazikitsidwa. Inu simukanakhoza kupeza nyumba yapafamu yoti mukhalemo, mzinda wawung'ono wa Jonesboro. Ndipo anthu akubwera kuchokera mailosi, atanyamula

nyali, akuyenda kudutsa mnkhalango, akukwera a—basi ndi kumabwera.

⁴⁸ Ine ndinakhala kumeneko mchipululu usiku wina, ndikupemphera msonkhano usanayambike, ndipo ndinawona madona aang’ono akubwera ali ndi nsapato zawo ndi masitonkeni m’nkhwapa mwawo. Ndiye asanafike kumeneko, amaima ndi kumasasa fumbi kumapazi awo, ndi kumavala masitonkeni awo ndi—ndi—ndi nsapato, ndi—ndi kumapita mu msonkhano.

⁴⁹ Ndipo ine ndinawawona iwo atagoneka ana awo odwala pansu pa magalimoto akale a thonje, ndi kukhala pamenepo usana ndi usiku; atagwirizira mapepala ndi chinsalu pa iwo, pamene imavumba, namondwe akuwomba; osachoka pamalo awo, akudikirira kuti angolowa mkati mwa chipindacho.

⁵⁰ Kumeneko ndi kumene akhungu anali kupenya, ogontha anali kumva. Ndipo utumiki, usikuuno, uli mailosi handiredi kudutsa pamenepo, koma moto wa chitsitsimutso wazima.

⁵¹ Kuwawona anthu akuyenda kumeneko ndi kuti... Ingolozani chala chanu, ndikuti, “Chabwino, kodi inu mukukhulupirira, m’bale?” Ndizo zonse, iye anali atatuluka ndipo atapita. Ndizo zonse zomwe zimayenera kuchitika. Iwo anakhulupirira. Chitsitsimutsocho chinali chikusuntha.

⁵² Tsopano, ophunzira awa anali atawona zimenezo, ndipo mmawonekedwe awubwana iwo anali akukhala ndi chisangalalo, pamene Yesu anali akupumula, pa zimene iwo anaziwona zikuchitika tsiku limenelo.

⁵³ Ndipo ine ndikuganiza chitsitsimutso chikuchita chinachake chonga chimenecho, kuti ife tsopano tikungokhala mu nthawi ya bata, pamene Iye akupumula mwinamwake pakati pa misonkhano, kapena chitsitsimutso ndi Kudza Kwake. Ndipo ife tikukondwerera zinthu zimene taziwona zikuchitika mu nthawi ya chitsitsimutso ichi, ntchito zazikulu ndi zodabwitsa. Ziribe kanthu zomwe dziko likunena, ife tikuziwonabe izo zikuchitidwa! Ndi neno, ndi zoono, izo zinachitika.

⁵⁴ Iwo ayenera kuti anatenga mwayi, pamene amayenda bwino bwino ndithu, kuti aziyankhula za Iye, za zochita Zake, za zodzinenera Zake, za Umesiya Wake. Ambiri a iwo ayenera kuti... mwa ophunzira awa, mwinamwake ankayankhula za zimene iwo anali ataziwona zikuchitidwa, wina ndi mzake.

⁵⁵ Chimodzimodzi monga momwe ife timachitira, mu nthawi ya chitsitsimutso ku Shreveport, pa nthawi ya chitsitsimutso ku—ku mzinda wina, ife timakambirana za zimenezo.

⁵⁶ Tsopano umo ndi momwe iwo anali kuchitira. Mwinamwake anali Simoni, monga ife tinakambira usiku wathawu, akuti, “Chabwino, pamene Andreyana andiuza ine za Iye, ine ndinali wokaikira pang’ono pokha. Koma pamene Iye anandiuza ine

yemwe ine ndinali ndi omwe bambo anga anali, izo zinachotsa kulingalira konse kwa ine. Ine—ine ndinakhulupirira izo pamenepeo.”

⁵⁷ Zikhoza kukhala kuti mwinamwake Filipino ananena, wina kapena winayo; mwinamwake anali Andreyana ananena. Iye tinayankhula za dona pa chitsime, usiku wathawu. Mwinamwake anali akuyankhula za iyeyo, pamene iwo ananena chinachake chonga ichi, “Abale, inu mukudziwa, pamene nthawi yanga yachirendo inali, pamene ine—tinapita kukagula zitumbuwa zina. Ndipo tinabwerera ndipo tinali titayima panja mtchire, ndipo tinamuwona Iye akuyankhulana ndi mkazi wa mbiri yoyipa uyu. Ife tinaganiza, m’mitima mwathu, ‘Bwanji ngati ena a ansemble atabwera nkudzaziwona izi, Mbuye wathu akuyankhulana ndi mkazi wakhalidwe limeneli, kodi iwo anganene chiyani za Iye?’ Ndiyeno ife tikukumbukira momwe ife timadziwira, amene anali ndi chidaliro mwa Iye, kuti izo zinali kwa cholinga china chimene Iye amayankhula kwa iye.

⁵⁸ “Ndiyeno pamene Iye anamuza iye, ‘Pita ukatenge mwamuna wako ubwere naye kuno.’ Ndipo iye anati: ‘Ine ndiribe mwamuna.’ Momwe mitima yathu inalumphira, chifukwa ife tinaganiza kuti nthawi imeneyo tinali ndi cholephera. Yesu anali atamuza mkaziyo kuti iye amayenera, apite akatenge ‘mwamuna wake,’ pamene iye analibe mwamuna. Inu mukukumbukira kuyang’anizana kumene tinali nako pankhope ya wina ndi mzake pamene ife tinkadabwa, kuganiza kuti chidaliro chonse chomwe tinali nacho mwa Iye, ndipo apa chinangogwa mwadzidzidzi?

⁵⁹ “Ndiye ife tinapeza, nthawi yomweyo Iye anayankhula anati, ‘Iwe wanena zooni, pakuti wakhalapo nawo amuna asanu, ndipo amene uli naye pakali pano si wako.’

⁶⁰ “Ndiye pamene iye anamuzindikira Iye pamenepeo ngati Mesiya, Mesiya wa Mulungu, ndipo ananena pamenepeo, kuti, ‘Ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera. Inu muyenera kukhala Mneneri, pakuti ife tikudziwa, pamene Mesiya adzadzaza, Iye adzachita izi.’ Ndipo umboni mu mzinda umenewo, umboni wa mkazi uja unali ndi anthu a mu mzindawo.”

⁶¹ Ndiye mwinamwake anali Yohane wachichepereyo yemwe anati, “Inu mukudziwa, ine ndikuuzani inu chimene chinapangitsa icho kukhala chenicheni kwa ine, tsiku lijali pamene Iye ananyema mkate. Tsopano, ife tonse tinali ndi njala, ndipo Iye anali atapita ku chipululu, ndipo sitimamupeza Iye, ndipo kumeneko ife tinakomana naye Iye. Ndipo makamau onse anadza pozungulira, ndipo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, ife tinamupeza Iye akuti, ‘Atumizeni iwo ku mzinda, kuti akatenge chakudya china.’ Ndipo—ndipo Iye anatiuza ife kuti ‘tiwadyetse iwo’ pamenepeo. Ndipo Iye anatenga masikono asanu amenewo ndi tinsomba tiwiri tating’ono, ndipo

Iye ananyema mkate umenewo. Ndipo ine ndinazindikira dzanja Lake pamene Iye amakhoza kubwerera kuti akapeze chidutswa china cha mkate, sikono imeneyo inali itameranso. Ndiyeno pamene Iye anafikiranso, nkuyika izo m'mbale, kenako nkufikiranso, nsomba imeneyo inali itameranso. Osati kokha nsomba wamba, koma iyo inali nsomba yophikidwa, mwaona, inali itameranso kale.

⁶² “Kodi ndi atomu ya mtundu wanji yomwe Iye anali ataimasula, abale, nsomba yophikidwa, mkate wophikidwa, kulambalala kumera? Ndipo ife tinadziwa kuti Iye anali Mlengi, koma apa Iye akupanga chirengedwe cha nsomba yophikidwa kale ndi mkate wophikidwa.”

⁶³ Yohane ayenera kuti ananena chinachake chonga ichi. Iye anati, “Inu mukudziwa, pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, ife tinkakhala kufupi ndi Yeriko. Ine ndikukumbukira kuti amayi anga Achiyuda anakonda kundigwedeza kuti ndigone masana; kugona kwanga kwa madzulo. Ine ndinkakonda kuwayang’ana mmaso mwawo, ndipo ankandiuza ine nkhani za m’Baibulo.”

⁶⁴ Ndipo, inu mukudziwa, icho ndi chinthu chabwino kuti mayi aliyense azichita kwa mwana wake. “Kumulera mwana m’njira imene ayenera kuyendamo.” Izo zingakhale zabwino kusiyana ndi kuyatsa televizioni ndi kuwonera zina za izi pano zomwe zikuyatika pa televizioni. Inu mungachite bwino ngati mutamuwerengera iye nkhani ya m’Baibulo, chifukwa imakhutitsa maganizo ake aang’ono.

⁶⁵ Tsopano anati, “Ankakonda... Iye anakonda kumandiuza ine za—nkhani ya mkazi wa ku Shunemu akumulandiranso mwana wake wamng’ono wamoyo, kudzera mwa mneneri Eliya. Ine ndinkazikonda zimenezo. Ndiye anakonda kumandiuza ine za anthu athu akubwera kuchokera ku Igupto. Ndipo ife tinali pa mtsinje wa Yorodani. Ndipo amakhoza kuloza kutsidya kwa mtsinje, ndi kumati, ‘Yohane, iwo anamanga msasa mbali inayo. Ndipo iwo anali zaka forte mchikululu chimenecho, ndipo Mulungu ankawadyetsa iwo mana. Zovala zawo sizinkaperepeseka nkomwe. Ndipo Mulungu ankawapatsa iwo mkate, watsopano, m’mawa uliwonse.’

⁶⁶ “Ndipo momwe mtima wanga wawung’ono, wachibwana, ndinkakonda kunena kuti, ‘Amayi, kodi Mulungu ali ndi mauvuni aakulu kwambiri kumwamba uko mu mlengalenga, ndipo Iye amawotcherako mkate wonse uwu, ndipo amawakonzekeretsa Angelo Ake kuti abwere nawo mkate wa m’mawa ndi kudzawuyika iwo pa...?’

⁶⁷ “‘Ayi,’ iwo amakhoza kunena kuti. ‘Yohane, ndiwe wamng’ono kwambiri kuti ungamvetse. Mwaona, Mulungu alibe mauvuni mu mlengalenga. Iye samasowa mauvuni. Ife tiyenera kukhala ndi mauvuni. Koma Mulungu samawasowa

iwo, chifukwa Iye ndi Mlengi. Mwaona, Iye amangoyankhula, ndipo mkate umangoyikidwa pamene. . . Iye ndi Mlengi.’

⁶⁸ “Ndipo, abale, pamene ine ndinayima pamene lero ndi kumuwona Iye akutenga chidutsa cha mkate chija ndi kuwunyema iwo, ndipo pamene Iye anafikiranso kwa chidutsa china, icho chinalengedwa, ine ndinadziwa kuti ife sitinali kutsatira—kutsatira mneneri wabodza. Ameneyo anali Mlengi, Mwiniwake, mwa Munthu.” Ndipo a . . .

⁶⁹ Ndiye mwinamwake iwo amakambirana maganizo a anthu ena; ena amakhulupirira, ena samakhulupirira; komanso maganizo Ake kwa anthu.

⁷⁰ Tsopano, inu mukudziwa, Chikhristu chasintha kwambiri, mmasiku otsiriza ano. Tsopano umayenera kumupembedzera munthu, kuwalonjeza iwo zambiri, kuwapatsa iwo zambiri, kuti muwapangitse iwo kukhulupirira, kubwera ku tchalitchi, ndi kuwalonjeza iwo kuti iwo adzakhala ndi oyanjana nawo abwinoko ndi chirichonse. Chimenecho si Chikhristu.

⁷¹ Chikhristu si kupembedzedwa. Chikhristu ndi kuvutikira. Kulondola. Ndi a—ndi a—a . . . Chikhristu si chomera chobzalidwa nkanyumba.

⁷² Chomera chobzalidwa nkanyumba, makamaka. Kuchita kumaipopera iyo nthawi zonse, kuying’itsa tizirombo pa iyo. Zimenezo zimakhala chifukwa cha kufowoka kwake. Ndipo umo ndi momwe umayenera kuchitira Akhristu ambiri, kukhala ngati ukuwapopera iwo ndi—malonjezano ambiri.

⁷³ Inu, simumasowa zimenezo. Chomera chenicheni chathanzi sichimasowa kupoperedwa kulikonseko. Tizirombo timathawira kutali kwa icho.

⁷⁴ Ziri monga ngati, lero, munthu uja akuyesetsa kutenga zinthu ndi kuzipotoza izo. Mulungu, pachiyambi, Iye anati, “Mulole mbewu iliyonse ibale mwa mtundu wake.”

⁷⁵ Ine ndinali kuwerenga mu *Reader’s Digest* apa, pamene iwo—iwo akutenga chomwe timachitcha chimanga cha haibridi, ndipo icho chimakhala ndi khutu lokongolako, zedi, khutu lalikulu kwambiri labwino; koma icho si chabwino, kulibeko kanthu kwa icho. Ndipo amapanga tomato wabwinoko, iye samakoma nkomwe ngati tomato, ndipo akupanga, ali ndi nkukhu tsopano yomwe ilibe nkomwe mapiko. Haibridi! Mukuona?

⁷⁶ Ndipo tsopano, kumbukirani, mukhoza kukhala ndi chimanga cha haibridi, koma simungakhoze kubzalanso mbewu imeneyo. Iyo siyingadzibalenso kachiwiri. Iyo idzafa. Chifukwa chiyani? Iyo ilibe moyo mmenemo. Inu mumayenera kuyipanga haibridi nthawi iliyonse. Ngati ikanakhala kuti si choncho, bwenzi ikumadzichulukitsabe. Zimenezo zimasonyeza kusinthika kuja, malingana ndi malingaliro a munthu, ndi zolakwika.

⁷⁷ Inu mukhoza kutenga a—kavalo wamphongo ndi kavalo, ndi kuzikweranitsa izo pamodzi ndi kupezapo bulu, koma bulu sangakhoze kudzibalanso yekha kachiwiri. Izo zatha. Ndizo zonse. Iye watha.

⁷⁸ Ndipo iwo akumanena tsopano, kuti mu zaka zina twente, ngati sawaletsa anthu awa kuti asamadye zinthu za haibridi izi, monga chimanga ndi tirigu ndi zinthu zomwe iwo akuzichita haibridi, kuti, “Zikusintha—kaimidwe ka akazi. Iwo samadzatha kukhala ndi ana, mu zaka twente kuchokera pano. Izo zikupha m’badwo.” Izo ziribe zinthu mwa izo.

⁷⁹ Munthu sakupangidwa monga ankapangiridwa kale. Tamuonani munthu lero. Bwanji, iwo, poyamba zinkakhala kuti, masewero a mpira anali ankanza. Tsopano amayenera kuvala zipewa; akumapha dazeni chaka chirichonse, akagundana pa mitu yawo ngati nkhwali, iye akumafera pomwepo tsopano; ndewu ndi chirichonse. Munthu anapangidwa ndi mulu wa matope. Ndi zimenezo, ndipo ndi chifukwa cha zinthu za haibridi, ndipo zavunditsa dongosolo lonse la—za moyo wathu, chuma chathu chonse.

⁸⁰ Ndipo—ndi—ndipo kusakaniza kumeneko kwalowa mu mpingo, aponso. Mmalo mokhala ndi gulu lenileni lolimba la okhulupirira Baibulo, iwo asakaniza izo ndi zipembedzo. Ndipo iwo ayenera kutero, “Ine ndiri ndi *ichi*, ine ndiri ndi *icho*; ndipo ine ndine wa *ichi*, ndipo ine ndine wa *icho*.” Ndi haibridi, ndipo chinthucho sichingathe kudzibalanso chokha.

⁸¹ Ife tikusowa Bukhu la Machitidwe kachiwiri. Koma njira yokhayo imene inu mungachitire zimenezo ndi kubwerera ku Baibulo, ndi kuchokako ku zina za chipembedzo cha haibridi izi.

⁸² Kusakaniza, kumachita kunyengereredwa! Wopanda chikhulupiriro! Basi gulu la—wa zofuka za ufa, basi kumangosisitidwa, kuchita kunyengereredwa kuti alowemo. “Ndine...” Ine ndikuti, kodi ndinu Mkristu? “Ndine wa Methodist.” Kodi ndinu Mkristu? “Ndine wa Presbateria. Ndine wa Chipentekoste.” Zimenezo sizikutanthauza *izo*, kwa Mulungu. [M’bale Branham anakhwatichitsa zala zake—Mkonzi].

⁸³ Ndinu Mkristu chifukwa munabadwira mu Mzimu wa Khristu, ndipo Mawu a Mulungu amakhala mwa inu.

⁸⁴ Inu mukudziwa, nthawizonse ndimakonda kavalo wowededwa kwambiri. Inu mukudziwa, amakhala ndi nzeru. Inu mukhoza—inu mukhoza kumuphunzitsa iye zinthu, kumamuchitira iye zinthu, ndipo iye amaphunzira. Koma mumutenge bulu wakale, inu simungakhoze kuchita kanthu kwa iye. Iye ndi bulu wamkulu wakale wamakutu aatali. Iye amakhala pamenepo, ndipo, inu mukhoza kuyankhula naye iye, iye amatukula makutu ake, ndipo, “Huh? Huh? Huh?” Mwaona, kuti, iye ndi haibridi basi.

⁸⁵ Zikundikumbutsa ine, zambiri za otchedwa Akhristu awa, haibridi, chipembedzo cha bulu. Iwe ukawawuza iwo Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; amati, “Ine sindimazikhulupirira Zimenezo.” Mukuona? Ndipo kotero iwe sungakhoze konse kumuphunzitsa iye kanthu. Iwe ungamuphunzitse bwanji iye; iye wapita, mulimonse. “Mpingo wanga umakhulupirira Iwo mwanjira *iyi*. Wanga umakhulupirira Iwo mwanjira *iyi*.” Koma Mawu a Mulungu amati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Ine sindimakonda Mkhristu wa haibridi.

⁸⁶ Ine ndimakonda a—kavalu wachibadwidwe. Iye amadziwa omwe abambo ake anali, omwe amayi ake anali, omwe agogo ake aamuna ndi agogo ake anali. Iye amadziwa mibadwo yonse kuyambira mmbuyo.

⁸⁷ Chomwechonso Mkhristu wachibadwidwe, iye amadziwa Amene Atate ake ali. Iye anachokera kwa Mulungu; Iye ndi Mawu a Mulungu, Iye ali yemweyo monga Iye wakhala ali nthawizonse. Iye ndi wachibadwidwe weniweni wa Mulungu, Mawu a Mulungu ali mwa iye, Yesu Khristu akudziwonetsera Yekha.

⁸⁸ Gulu la osakhulupirira! Yesu ankafuna kugwedeza gulu la tizirombo tsiku lina, Iye anali ndi ambiri akumutsatira Iye. Iye anali ndi ophunzira Ake. Kenako, Iye anali nawo sevente aja, bungwe la azitumiki. Kenako, Iye anali ndi osonkhana, mwa zikwi. Ndiyeno Iye anapanga neno ili, Iye anati, “Kupatula mutadya Magazi... kudya thupi la Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake, inu mulibe Moyo mwa inu.”

⁸⁹ Tsopano kodi inu mukuganiza kuti dokotala wazamankhwala anganene chiyani, atakhala uko mwa osonkhana? Kodi mukuganiza kuti munthu woganiza bwino angatani, zimene ife timadzitcha kuganiza mwanzeru? Iye sanazifotokoze konse izo. Iye sankasowa kuti azifotokoze izo. Chifukwa chiyani, dokotala anganene kuti, “Chokani kwa Munthu ameneyo. Iye wapenga. Iye... Ife tikhala odyana anthu. Kumwa Magazi a Munthu, kudya mnofu Wake?”

⁹⁰ Ndipo osonkhana, ine ndikulingalira wansembe anati, “Nthawi yake ndi inoyi. Apa ndi pamene ife tikubweramo. Ife tatuluka! Ife sitidzapezeka nkomwe pa wina wa misonkhano.” Iwo anapita. Kenako, Iye anawachotsa onsewo kwa Iye.

⁹¹ Kenako Iye anapotoloka ndipo Iye ananena kwa seventewo, Iye anati “Kodi inu mudzanena chiyani pamene mudzawone Mwana wa munthu akukwera Kumwamba kumene Iye anachokerako?”

⁹² Tsopano, sevente amenewo anati, “Mwana wa munthu kukwera kumene Iye anachokerako? Bwanji, Iye wakhalapo nafe ife modyera ziwetomo mmene Iye anabadwiramo. Ife tikuwadziwa amayi Ake. Ife tinaziwona zovala, nsalu ya

pa joko zimene Iye anakulungidwamo. Iye anabadwira uko mu Betelehemu wa Yudeya. Iye analeredwa cha kuno ku Nazareti. Abale Ake ndi amenewo, azilongo Ake, ndi onse a iwo tiri nawo. Ndiyeno Iye anati, ‘Mwana wa munthu Uyu adzakwera mmwamba?’” Tsopano, Iye sanachifotokoze chimenecho, Iye anangochinena icho. Tsopano, iwo sanakhoze kuzifotokoza izo, iwo sakanakhoza kuzikonza izo mmalingaliro awo. “Chabwino,” iwo anati, “apa ndi pamene tikulowerapo,” kotero iwo anatuluka. Ndizo momwe iwo akanakhoza kupiririra.

⁹³ Iwo akadali nawobe magulu omwewo. Uko nkulondola. Ife tikadakali nawobe iwo. Ife tikuzindikira.

⁹⁴ Kenako Iye anapotoloka. Kumbukirani, ophunzira amenewo sakanakhoza kufotokoza zimenezo, nkomwe, koma iwo anali nacho chikhulupiriro. Pamenepo Yesu anapotoloka ndipo anayang’ana kwa khumi ndi awiriwo, ndipo anati, “Kodi inunso muzipita?”

⁹⁵ Kenako Petro ananena mawu ochititsa chidwi awo: “Ambuye, tingapitenso kuti? Pakuti ife tiri okakamizika kwathunthu, ife tikudziwa kuti Inu muli nawo Mawu a Moyo, ndipo Inu nokha.” Mukuona? Iwo sakanakhoza kufotokoza momwe iwo akanati adyere thupi Lake ndi kumwa Magazi Ake. Iwo sakanakhoza kumvetsa momwe Iye akanati adzakwerere kuchokera kumene Iye antsikirako, pamene Iye ankadwira mu Betelehemu. Iwo sakanakhoza. Koma, mwaona, chikhulupiriro sichimadziwa kulephera kulikonse. Icho ndi chozikika. Icho chimakhala pamenepo, ziribe kanthu zomwe chirichonse chinanena. Icho chinakhala pamenepo. Iwo anadzedwera ku Moyo uwu. Ndipo Iye. . . Iwo anakhala pamenepo.

⁹⁶ Tsopano mitundu yosiyanasiyana imeneyo. Ena anakhulupirira. Ena anati, “Munthu sanalankhulepo monga chonchi.” Ena sanakhulupirire, ndipo iwo anati, “Oh, izo, mwina anakambirana zimenezo.”

⁹⁷ Ena anati, “Palibe munthu anayankhulapo monga Munthu uyu. Pali chinachake chachilendo cha Iye. Zimene Iye amanena, Iye amakhoza kuziyikira kumbuyo.” Chabwino, iwo ananena zimenezo, inu mukudziwa, anati, “Iye samayankhula ngati wansembe. Iye samayankhula ngati rabi. Pakuti zimene Iye amanena, Mulungu amaziyikira kumbuyo, Iye amatsimikizira zimene Iye amanena.” Oh, mai!

⁹⁸ Ayenera kuti anali Yohane wamng’ono, ndiye, anati, “Taganizani za zimenezo! Ife tiri naye Iye limodzi nafe pakali pano. Zimenezo ziyenera kuti zinali chitonthozo bwanji! Ndi chitetezo bwanji!” Chiyenera kukhala chitetezo bwanji kwa ife!

⁹⁹ Ndine wa misonare, ndazungulira ndi kuzungulira dzikoli lapansi. Ndipo ine ndawonapo mitundu yonse ya zipembedzo ndi mitundu yonse ya milungu imene iwo ali nayo, milungu yachikunja; Achimuhamadi, Achibuddha, ndi Asikhi, Jain, oh,

chirichonsecho, ndi milungu yachikunja ya anthu a mafuko. Koma, aliyense wa iwo, palibe mmodzi wa iwo wolondola koma Chikhristu. Aliyense wa iwo, oyambitsa awo anafa, ndipo iwo anali nawo manda kumene iye anakaikidwako. Koma Chikhristu ndi chimodzi chokhacho cholondola, chifukwa Woyambitsa wathu anafa, anaikidwa m'manda, koma anaukanso, ndipo tikhoza kutsimikizira kuti Iye ali wamoyo.

¹⁰⁰ Pa manda a Muhammadi, kwa zaka zikwi ziwiri zapitazi, pafupifupi, kwakhala kuli kavalo woyera, kumasintha azilonda maora ambiri aliwonsewo, kuyembekezera Muhammadi kuti adzawuka kwa akufa ndipo adzakwera kudutsa dzikoli ndi kudzaligonjetsa ilo.

¹⁰¹ Koma Yesu anawuka kale kwa akufa, wakhala ali mmwamba kwa zaka zikwi ziwiri, ndipo ali nafe usikuuno. Ndiyeno pamene ife tiwona mdima, ndi kuwona mapeto a nthawi, momwe izo zikuchitikira tsopano, kubwera ku maora amene ife tikukhalamo, pamene ife tikuyenda pa njira yaikulu ya moyo, kumene nyanja yamkuntho, ndi—ndipo chombocho chikhoza kusweka nthawi iliyonse, nyali zazing'ono izi zitha kuzima monga *choncho*. [M'bale Branham anakhwatichitsa zala zake—Mkonzi]. Kapena, ife mwina sitichoka mchipinda chino usikuuno, palibe aliyense wa ife. Ife sitikudziwa nthawi yomwe imfa ingabwere.

¹⁰² Ndipo kuyenera kuti kunali kumverera kotetezeka bwanji, kwa ophunzira amenewo, kudziwa kuti Mlengi yemweyo, yemwe anali atadzizindikiritisa Yekha bwinobwino kuti anali Munthu ameneyo, anali akuyenda nawo panyanja.

¹⁰³ Ndi lingaliro lodala bwanji, icho ndi chiyembekezo chodala bwanji, ndi chitsimikizo chotani chomwe chiri, mu nthawi yamdima ino kumapeto kwa mbiriyakale ya dziko lapansi, kudziwa kuti Mlengi akuyenda nafe panjira yofunika ya moyo, titalongezedwamo motetezeka! Mabomba, chirichonse chimene chingabwere, iwo akwere, kuphulika, kuwomba, chirichonse chimene iwo akufuna, izo sizimapanga kusiyana kulikonse kwa ine, ine ndikuyenda ndi Mlengi. Ndi chitetezero bwanji, pamene tikuyenda mmadzi awa!

¹⁰⁴ Tsopano pamene anali kuyankhula, kuyankhula za Iye, za zinthu zazikulu zimene Iye anachita. Pambuyo pa phwando la chitsitsimutso, Yesu mwinamwake anali akupuma monga Iye akuchitira, ine ndinati, pakati pa zitsitsimutso. Ndipo ife...iwo anali atazindikiritidwa momveka kwambiri kwa Yemwe Iye anali. Anthu ankadziwa Yemwe Iye anali, mwa iwo omwe Iye anali kuwachititsa khungu. Koma iwo amene anali ataligwira Lemba, chifukwa iwo ankadziwa kuti Lemba... Mawu a Mulungu aperekedwa, mochuluka, kwa m'badwo uliwonse, ndipo lonjezo limenelo la m'badwo umenewo liyenera kukwaniritsidwa. Ndipo Iye anakwaniritsa ndendende zomwe

zimayenera kuchitidwa mu nthawi ya Mesiya. Iye anakwaniritsa choyenera chirichonse. Ndiye ife . . . iye anatsimikiziridwa kuti Iye anali Munthuyo.

¹⁰⁵ Koma, inu mukuona, Iye anali wa wamba kwambiri. Iye sankavala monga wansembe. Iye anali, ayi, wosaphunzira monga—monga zomwe tingadzitche maphunziro. Ife tiribe umboni wa Iye ngakhale kuti ankapita ku sukulu. Koma panali chinachake chokhudza Iye chimene chinali chosiyana.

¹⁰⁶ Ndiyeno Iye anawaitana iwo, pamene iwo samamvetsa, anati, “Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mukuganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo ndicho chinthu chimene chimachitira umboni za Ine. Iwo akuuzani inu Yemwe Ine ndiri.”

¹⁰⁷ Ndipo tsopano, kumbukirani, iwo onse anali nazo izi mu mtima mwawo ndipo anali akuganiza za zinthu izi. Ndipo pamene anali akuyenda pa nyanja, momwe iwo amakhalira ngati ana, bola ngati Iye ali mu ngalawa ndi iwo.

¹⁰⁸ Tsopano, mzanga, chimenecho chiyenera kuchita chiyani kwa ife! Yesu Khristu yemweyo wozindikiritsidwa, Mlengi yemweyo, Mulungu yemweyo, ali ndi ife usikuuno. Ndi chitetezero bwanji—ndi choncho, ndi kumverera bwanji, kudziwa kuti Kukhalapo Kwake kuli pano.

¹⁰⁹ Tsopano ife tikupeza, pamene iwo anali ndi nthawi yopambana iyi, zonse mwadzidzidzi, vuto linadzawuka. Ngalawayo inayamba kupendekeka, matanga anaphulika, madzi anadzaza mngalawamo. Ziyembekezo zonse za kupulumuka zinali zitapita.

¹¹⁰ Tsopano, kodi sizodabwitsa, chimodzimodzi monga momwe zikukhalira tsopano, pamene ife tikufika kumapeto tsopano, kodi sizodabwitsa? Ife tikhoza kuyankhula za momwe Iye aliri wamkulu; ife tikhoza kudziwa momwe Iye aliri wamkulu, mu mpingo wathu pamene ife tichitira umboni; ife timawauza athu—antchito athu, olemba ntchito, momwe Iye aliri wamkulu; ife timawauza athu pa msewu momwe Iye aliri wamkulu; ndipo, pamene mavuto afika, ife timakhumudwa. Mukuona? Ife basi. . . Mukuona? Zinthu zimene ife tinamuwona Iye akuchita, zinthu zimene ife timadziwa kuti Iye amachita; ndi mungolola matenda aang’ono, kapena vuto laling’ono likanthe mnyumbamo, muwone zimene zimachitika; zonse zimapita mzdutswa, zonse—ziyembekezo zonse zimapita.

¹¹¹ Ngakhale iwo anamuwona Iye akuchita zinthu zambiri; zonsezo zinaiwalika pamene vuto linadzakantha.

¹¹² Monga tsopano, ife tachiwonapo chitsitsimutso chachikulu ichi, tiri nayo mbiriyakale ya zitsitsimutso zina zazikulu, ife tiri nako Kukhalapo Kwake, ife timazidziwa zinthu izi, ndipo nthawizina vuto limayamba limene ife sitingathe kulithetsa. Iwo. . .

¹¹³ Mwa chitsanzo monga tsopano, ife tiri ndi vuto mmipingo yathu tsopano. Ife timakhala nawo mavuto achipembedzo, mikangano mmipingo yathu. Ife sitimadziwa chomwe chiti chidzachitike. Ife timawona chinthu chachikulu chikupangika kumeneko. Tonse a ife okhulupirira mu Baibulo timawona chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Palibe wina koma amene akudziwa zimenezo.

¹¹⁴ Ndipo mipingo yonse ibweretsedwa mu Bungwe la ecumenical la Matchalitchi. Ndiye, pamene mudzachite zimenezo, inu mudzataya chiphunzitso chanu chachikulu cha uvangeli cha Baibulo. Ndipo Achipentekoste akuzimvera chifundo zimenezo, akupita mpaka mmenemo, monga nkhumba ikupita kuti ikaphedwe, ndiko kulondola, bungwe la ecumenical. Atsogoleri ambiri Achipentekoste akugwirizana nawo iwo. Ine ndikukuuzani inu, musadzazike konse khosi lanu mu chinthu choterocho. Ndizo ndendende zomwe Baibulo linati zikanadzachitika. Ndi chimenecho chirombo ndi chilemba, ndipo, mwangwirowo, chirichonse chayikidwa bwino mu dongosolo, ndipo tikuziwona izi ndipo ife tikudabwa chomwe chiti chidzakhale chotsatira chake.

¹¹⁵ Vuto linayambika. Ndipo iwo anayiwala kuti Mmodzi yemweyo yemwe iwo anali kumukamba, Mlengi yemweyo, anali mu ngalawa limodzi nawo.

Tsopano inu mukuti, “Ngati ndingakhoze kuganizira zimenezo!”

¹¹⁶ Chabwino, kumbukirani, ife tikanali nayebe Iye, chifukwa Iye ndi Mawu, nthawizonse. Mu Yohane 1:1, monga ife tinayankhulira usiku wathawu, “Iye anali Mawu; ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhazikika pakati pathu.” Ndipo ife tikadali nawobe Mawu Ake amene amatilondolera ife ku maganizo Ake ndi zochita Zake za tsiku lino. Mukuona? A... Osati maganizo amene Mose anali nawo mu tsiku lake, osati maganizo a ophunzira, osati maganizo a Luther, kapena Wesley, kapena m’badwo wa Pentekoste, kapena chirichonse cha izo. Ife tiri nalo Baibulo apa limene limatiuza ife zimene zidzachitike tsopano. Mukuona? Ife tikuwona chitsitsimutso cha Chipentekoste mu Baibulo, Chilutera, ndi mibadwo yonse ya mpingo imeneyo. Ife tinawawona iwo. Koma ifenso tiri nalo Lemba pano limatiuza ife chimene chiti chidzakhale tsopano. Ndipo ameneyo ndi Mulungu, Mulungu akutanthauzira Mawu Ake Omwe a m’badwo uno umene ife tikukhalamo. Iye ndi wodzitanthauzira Iye Mwini. Ndipo, komabe, ife timakhumudwa. Musati muzikhumudwa.

¹¹⁷ Ophunzira ake nthawizina amakumana ndi zovuta zakuthupi zomwe sangathe kuzithetsa, monga matenda, khansa, zina zotero, zomwe madokotala sangakhoze, samadziwa

choti achite nazo. Ifenso, monga iwo, timayiwala Amene ali m'ngalawa.

¹¹⁸ Iwo ankayenera kudziwa kuti Iye ankadziwa zinthu zonsezi. Iye ankadziwa kuti izo zikanadzachitika. Iye anali...Iye ankadziwa zinthu zonse, chotero Iye ankadziwa kuti zimenezi zidzachitika. Izo zidzachitika kwa iwo. Nchifukwa chiyani Iye anazilola izo kuti zichitike? Pamene Iye analowa mngalawa imeneyo, Iye ankadziwa kuti zimenezo zichitika.

¹¹⁹ Iye amadziwa kuti ife timayenera kudzakwaniritsa chochitika ichi, ndipo Iye anatiuziratu ife mu Baibulo kuti izo zikanadzakhala mwanjira imeneyo.

Tsopano kodi Iye anali kuchita chiyani? Kuyesa chikhulupiriro chawo.

¹²⁰ Nchifukwa chiyani Iye amalola a—a—mkazi wabwino, wamng'ono, wowoneka ngati mayi kumakhala mchikuku, monga choncho? Nchifukwa chiyani Iye amalola anyamata abwino apa, anyamata aang'ono awa akhala pano mu zikuku izi, madona, ndi ena otero? Nchifukwa chiyani Iye? Ndipo, komabe, iwo akhoza kukhala olumala, nkumangokhala moyo wamba. Koma pakhoza kukhala ena akhala pano ali ndi vuto la mtima, ndipo, ngati Mulungu sakuchizani inu, inu mukhoza kukhala mutafa usanafike mmawa. Uko nkulondola. Iye ankadziwa kuti izo zikanadzachitika. Mwinamwake izo zimachitika kuti chikhulupiriro chathu chiyesedwe. Ndi chifukwa chake izo zinachitidwa kwa iwo. Iye ananena chomwecho. Mukuona? Chomwechonso tsopano.

¹²¹ Iye anali atatsimikizira Yemwe Iye anali, mwa Mawu ndi zizindikiro zomwe Iye anali atazitsimikizira pakati pawo, kuti Iye anali Mesiya wotsimikiziridwa, wodzozedwa yemwe anali nkudza.

¹²² Ndipo Iye watsimikiziridwa pakati pathu, mwa Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kubwerera kwa zinthu zomwe Iye analonjeza mu tsiku lino, zomwe Iye akanati adzazichite. Iye watsimikizira kuti Iye ali pano. Iye akutsimikizira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo mukuwona momwe mophweka ife timakhumudwira pa kanthu kakang'ono kalikonse? Tisamazilole kuti izo zizichitika. Ayi.

¹²³ Iye anati, “Ngati Ine sindichita ntchito zomwe zinalembedwa za Ine, ndiye musandikhulupirire Ine.” Ndipo ngati Mpingo, ngati Mzimu Woyera lero, sukuchita zinthu zomwe iwo unkayenera kuti udzachitire ora lino, ndiye musakhulupirire Uthenga; inu muli nawo ufulu kuti musawukhulupirire Iwo.

¹²⁴ Koma Iye analonjeza kuti zinthu izi zimene Iye akuchita pakali pano zidzachitika pa nthawi ino. Chotero izo ziyenera kutipangitsa kumva kukhala otetezeka, ndikuti, “Ndikupita ku msonkhano kumeneko. Mzimu Woyera wawukulu, ine ndikumvetsa, uli kumtundu uko ukuwulula zinsinsi za mitima

ya anthu.” Ndizo ndendende zomwe Iye anati Iye akanadzachita pamene Iye azidzawululidwa mmasiku otsiriza. Yesu Khristu ananena, Mwiniwake, kuti ndizo ndendende zomwe Iye akanati adzachite.

¹²⁵ Ndipo Iye anati, “Dziko likanadzakhala mu chikhalidwe monga linali mmasiku a Sodomu.” Ndipo ndi pamene ilo liri tsopano. Iye anati, “Mipingo idzalekanitsidwa, monga momwe inachitira nthawi imeneyo,” Loti, wofunda, uko mu Babeloni, kapena uko mu Sodomu, ndi Achisodomu. Iye anati, “Abrahamu, wosankhidwayo, gulu loitanidwa-atuluke,” ndipo Iye anatumiza wamthenga kwa gulu losankhidwalo. Ndipo Iye anatumiza atumiki awiri kumeneko kwa iwo, kuimirira mmodzi aliyense. Ndipo ndi chimenecho basi chimene Iye wachita, ngakhale ku dzina lililonse, kachitidwe kalikonse, kusuntha kulikonse, chirichonse mwangwiro basi, chizindikiro chirichonse, mawonetseredwe aliwonse, chimodzimodzi basi mofanana. Iye anati izo zikanadzachitika.

¹²⁶ Tsopano kodi ife tikuwopa chiyani? Kodi zinthu izi ziri pa ife izi nzachiyani? Iye akutiyesa ife, awone zomwe titi tidzachite nazo. Muzindikire.

¹²⁷ Iye anawawuza iwo, anati, “Tsopano, ngati inu simungakhoze kundikhulupirira Ine, mukhulupire ntchito zimene Ine ndikuzichita; izo zikuchitira umboni wa Yemwe Ine ndiri.” Iwo ankayenera kudziwa zimenezo, koma iwo sanatero. Iwo . . .

¹²⁸ Iye anali Mulungu, Yemwe analenga, Mlengi wa mphepo ndi nyanja. Ngati Iye anakhoza kulenga mphepo ndi nyanja, kodi Iye sakanatha kuzipangitsa izo mochuluka kumvera Mawu Ake? Ngati Iye analenga chirichonse, kodi Iye sangapange chirichonse kuti chizimumvera? Tiyeni tizikumbukira, aponso, Iye analenga matupi athu, nawonso adzayenera kumvera Mawu Ake. “Chabwino,” inu mukuti, “ngati ine ndikanakhala wotsimikiza za izo.” Chabwino, ife tiri otsimikiza za izo. Iye ali pano kuti atsimikizire izo. Iwo ayenera kumvera izo. Kumbukirani. Iye ali nazo . . .

¹²⁹ Pamene ife tikugona, sikanthu koma mwina supuni yodzaza phulusa, Iye analonjeza kuti adzalidzutsa phulusa limenelo. Iye analonjeza kuti adzalidzutsa ilo. Thupi liyenera kumumvera Iye. Ndipo ndi pamene ife tifa, ife timakhala otsimikiza kuti ife tidzaukitsidwa, chifukwa Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita zimenezo. Ndipo lonjezo Lake ndi Mawu Ake, ndipo ife timakhulupirira. Inu mumakhulupirira mu chiukitsiro cha thupi? Ndithudi. Ngati simutero, inu sindinu Mkhristu. Chotero ife timakhulupirira kuti Iye adzatiukitsa ife pa masiku otsiriza. Iye analonjeza kuti adzachita zimenezo. Ndipo ndi chiyani chimenecho? Amenewo ndi Mawu Ake. Ndi pamene ife

timayika chirichonse chimene ife tiri nacho, pa Mawu amenewo pomwe.

¹³⁰ Ndiyeno pamene izo zifika ku nthawi imene ife tikuwona Mawu akuzindikiritsidwa, kuti akhale ndi ife; ndiye ife timakhala monga ophunzira, mu chochitika china pamene iwo anali pa nyanja, ndi—ndipo iwo anali pafupi kuti amire kachiwiri, mu chochitika china. Ndipo iwo anamuwona Yesu akubwera akuyenda pa madzi, ndipo iwo anachita mantha. Iwo anati, “Ndi—ndi chipukupuku. Ndi zowopsya.” Amawopa kuti unali mzimu, ndipo anafuula ndi mantha. Chinthu chokhacho chimene chikanawathandiza iwo, iwo anachita nacho mantha.

¹³¹ Ndipo chomwechonso izo ziri lero, chinthu chokhacho kumene chomwe chingakhoze kuwathandiza anthu, iwo akuchiwopa icho. Iye anati, “Musawope. Ndi Ineyo.” Iye amayankhula. Inu mungadziwe bwanji kuti anali Iyeyo? Iye amazindikiritsidwa ndi Mawu Ake. Umo ndi momwe Iye anazindikiritsidwira nthawi yoyamba. Umo ndi momwe Iye amazindikiritsidwira nthawi iliyonse, mwa Mawu Ake. Zindikirani.

¹³² Pambuyo pakuti awa ophunzi-...ophunzira anadzazipeza okha pamapeto, ziyenera kuti zinadzaziwika pa ena a iwo kuti Mlengi anali akadali nawo iwo.

¹³³ Ine ndikuyembekeza kuti izo zikuchita zimenezo kwa ife, usikuuno, pakuti Ahebri 13:8 amati Iye ali yemweyo.

¹³⁴ Ndiye kodi iwo anachita chiyani? Iwo anamudzutsa Yesu. “Pitani mukamudzutse Yesu. Mumudzutse Iye, mumuitanire Iye powonekera!” Iye amayitanidwa mophweka. Iwo anali atawona, anawona zinthu zambiri zimene Mulungu anachita, ndipo—ndipo—ndipo Mawu akumutsimikizira Iye. Chomwechonso ifenso tatero. Ndipo Iye sanali wovuta kuyitanidwa kuti achitepo kanthu.

¹³⁵ Iwo anamudzutsa Iye, ndipo anati, “Kodi Inu...Inu simukusamala kuti ife tikufa?”

Inu mukuti, “Kodi tingatsimikize bwanji za izi? Kodi tingatsimikizire izo?”

¹³⁶ Yohane 14:12, Yesu anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Ndizo ndendende. Chikhulupiriro chatu chikumubweretsa Khristu pamaso pathu.

¹³⁷ Iye ananena mu—mu Luka, mutu wa 17, “Mmasiku otsiriza pamene Mwana wa munthu azidzawululidwa, idzakhala nthawi yonga Sodomu ndi Gomora.” Ife tikuziwona zimenezo zikuchitika.

¹³⁸ Iye anati, nthawi imeneyo isanachitike, mu Malaki 4, kuti, “Padzakhala Uthenga udzapite umene udzawabwezeretse anthu kubwerera ku Chikhulupiriro chapachiyambi chimene

chinaperekedwa kamodzi kwa anthu.” Nthawizonse dongosolo la Mulungu lidzachita zimenezo. Ndiyeno oyipa adzakhala mapulusa, ndipo olungama azidzayenda pa mapazi awo.

¹³⁹ Iye tikuziwona zonsezi zikulonjezedwa. Iye akuyembekezera pakali pano kwa inu, inu, inu, aliyense wa inu, kuti mumuitanire Iye powonekera. Kumuitanira Iye powonekera! Ndiko kumene Iye akufuna kukakhalako, kuitanidwa pa malo antchito. Zindikirani pamene inu mumuitanira Iye powonekera, chotero kenako ife tingati, “Tiyeni timudzutse Iye.” Kenako, muitaneni Iye kuti atsimikizire Mawu Ake ndi a—chinthu chimene Iye analonjeza kuti adzachita, momwe Iye akanadzachitira. Ife tingadziwe, mu vumbulutso la Yesu Khristu mmasiku otsiriza, zidzakhala monga izo zinali mmasiku a Sodomu. Iye analonjeza vumbulutso limenelo kwa Mpingo, pamene Iye akanati adzawululidwe. Chotero musakaikire ndi kuwopa, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

¹⁴⁰ Ine ndinamumva mkazi, nthawi ina, pamene ine ndinali kuyankhula za Iye kukhala wamkulu kwambiri. Iye anati, “Pali chinthu chimodzi chimene ine ndiri nacho chotsutsa chiphunzitsa chanu, Bambo Branham.”

¹⁴¹ Ine ndinati, “Chabwino, zikomo inu, ngati muli ndi chinthu chimodzi chokhacho.” Ine ndinati, “Ine—ine ndikuyembekeza Mulungu amangochipeza icho mwanjira imeneyo.” Ndipo iye anati, “Chabwino, inu mumadzibwekerera kwambiri za Yesu.”

¹⁴² Ine ndinati, “Ine ndikuyembekeza kuti ndicho chinthu chokhacho chomwe chiri chonditsutsa ine.” Ndipo—ndipo ndinati, “Ine sindimabwekerera mokwanira za Iye.”

¹⁴³ Iye anati, “Oh, inde, inu mumatero.” Anati, “Inu mumamupanga Iye Waumulungu.” Anali mkazi yemwe sankakhulupirira kuti Yesu anali Waumulungu. Iye anali wa Christian Science. Ndipo anati, “Inu mumamupanga Iye—inu mumamupanga Iye Waumulungu, mumamupanga Iye Mulungu.”

¹⁴⁴ Ine ndinati, “Iye ndi Mulungu, kapena wonyenga wamkulu yemwe dziko linayamba lamudziwapo.” Ine ndinati, “Iye. . .”

¹⁴⁵ Anati, “Chabwino, ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu, mwa Baibulo lanu, kuti Iye sanali. Iye anali mneneri chabe.”

Ine ndinati, “Iye anali mneneri, moona, koma Iye anali Mulungu, aponso.”

Anati, “Iye anali munthu ndipo Iye anali wachivundi.”

Ine ndinati, “Zimenezo nzoona, aponso.”

¹⁴⁶ Iye anati, “Panjira yopita kukaukitsa Lazaro kumanda, Yohane Woyera mutu wa 11, anati, Baibulo linati, ‘Yesu analira.’”

Ine ndinati, “Zimenezo nzoona.”

147 Iye anati, “Chabwino, izo zikutsimikizira kuti Iye sangakhale Waumulungu, ndipo nkumalira.”

148 Ine ndinati, “Oh, mai, dona, mkangano wanu ndi umenewo?” Ine ndinati, “Umenewo ndi wofooka.” Iye anati . . . Ine ndinati, “Zona, Iye anali Munthu pamene Iye anali kulira; koma pamene Iye anadzayika thupi Lake laling’ono kuti lisunthe, anakokera mapewa Ake aang’ono mmbuyo ndipo anati, ‘Lazaro, dzuka,’ ndipo munthu amene anali wakufa masiku anayi, ndipo anali akuvunda mmanda, anadzaima pa mapazi ake ndipo anakhalanso moyo, zimenezo zinali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu.”

149 Iye anali munthu, kunja kuno mu ngalawa iyi usiku umenewo, pamene Iye anali uko pa nyanja, kumene ziwanda teni sauzande za mnyanja zinalumbira kuti zikanadzamumiza Iye. Ngalawa yaing’ono yachikale ija inkapendekeka ngati chotsekera mabotolo kunja uko pa nyanja ya mkuntho. Iye anali munthu, atatopa, akugona. Koma pamene iwo anamudzutsa Iye ndi kumuyitanira Iye powonekera, Iye anaika phazi limodzi pa chingwecho ndipo anayang’ana mmwamba, ndipo anati, “Bata, khala chete,” ndipo mphepo ndi mafunde zinamumvera Iye. Ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu.

150 Iye anali munthu pamene Iye anatsika kuchokera pa phiri, wanjala, akuyang’ana pa mtengo kuti apeze chinachake choti adye. Iye anali munthu pamene Iye anali ndi njala. Koma pamene Iye anatenga masikono asanu ndi nsomba ziwiri, ndi kudyetisa zikwi zisanu, ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu mwa munthu ameneyo.

151 Munthu aliyense amene anapindulapo chirichonse cholozeka, akhala ali anthu amene amakhulupirira zimenezo. Kulondola. Wandakatulo ndi ena-ochuluka ankakhulupirira zimenezo, kuti Mulungu anali mwa Khristu, akudziyanjanitsa Yekha kwa dziko lapansi.

152 Ndipo tsopano Khristu ali mu Mpingo, akuyanjanitsa anthu kwa Mulungu. Iye analonjeza kuti adzachita zimenezo. Izo zinalembedwa kuti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Inu mukukhulupirira zimenezo? Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse, kuti Iye akungoyembekezera tsopano kuti ayitanidwe powonekera. Tsopano chinthu chokha chimene chingakhoze kumuitanira Iye powonekera, ndi kuti ife timudzutse Iye mwa ifeeni, timuitanire Iye powonekera.

153 Iye anali mphatso yaikulu kwambiri imene Mulungu anayamba walipatsapo dziko lapansi. “Mulungu analikonda kwambiri dziko lapansi kotero kuti Iye anapereka Mwana Wake wobadwa yekhayo; aliyense wokhulupirira mwa Iye asawonongeke; akhale nawo Moyo Wamuyaya.” Muwoneni

Mulungu ndi mphatso Yake. Tsopano, anthu ankaigwiritsa ntchito mphatso ya Mulungu.

¹⁵⁴ Mkazi wamng’ono, nthawi ina, iye anakhulupirira zimenezo, kuti Iye anali mawonetseredwe a Mulungu mthupi. Ndipo iye anati, “Ngati ndingakhudze chovala Chake, ine—ine—ine ndikhala wamphumphu.”

¹⁵⁵ Tsopano, iye anakhudza chovala Chake. Ndipo Iye anapotoloka, ndipo anati, “Ndani wandikhudza Ine? Mwaona, ukoma, mphamvu, zachoka mwa Ine.” Iye anakhudza chovala Chake. Zimenezo anali iye akugwiritsa ntchito mphatso ya Mulungu. Mukuona? Iye anafooka zitachitika zimenezo.

Koma pamene Iye anachoka kunyumba kwa Lazaro . . .

¹⁵⁶ Kumbukirani, Yohane Woyera 5:19, Yesu anati, “Indetu, indetu, Ine ndinena kwa inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awona Atate akuchichita.” Kumbukirani, Yesu Khristu sanachite konse chozizwitsa chimodzi, sanachite konse kalikonse mwanjira ya chazimu, mpaka poyamba Iye atawona masomphenya a choti achite. Ndi angati akukhulupirira kuti izo ndi zoona? Yohane Woyera 5, “Indetu, osati zimene Ine ndikumva, osati zimene wina wandiuza Ine; zimene Ine ndikuwona Atate akuchita, zomwezonso Mwana akuchita.” Tsopano ngati izo siziri chomwecho, ndiye Lembala lonselo siliri chomwecho. “Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangachite kalikonse mwa Iyeyekha; koma chimene Iye awawona Atate akuchita, chomwechonso Mwana amachita. Atate amagwira ntchito, ndipo Ine ndimagwira ntchito yomweyo.” Mwa kuyankhula kwina, Iye ankangozichita mwasewero, ankachita zimene Mulungu ankamuza Iye kuti achite.

¹⁵⁷ Tsopano, kumbukirani, pamene Iye anapita kuchoka kunyumba kwa Lazaro, Iye anali atapita masiku angapo. Lazaro anadwala, ndipo anamuitana Iye. Iye sanapiteko. Patapita masiku awiri, Lazaro anadwalika. Chotero iwo anamuitananso Iye, Iye apobe sanapite. Ndiye pamene nthawi yoikika, Atate anali atamuwonetsera Iye zimene zikanadzachitika, Lazaro anafa. Ndipo Iye anapotoloka, pamene Lazaro anafa, anati, “Lazaro wamwalira, ndipo Ndine wokondwera chifukwa cha inu kuti Ine sindinali kumeneko.” Iwo bwenzi akumufuna Iye kuti amupempherere iye, ndi zina zotero. Iye anangochita chimene Mulungu anamuza Iye kuti achite, chimene Iye anachiwona, masomphenya. Mwaona, Iye anali atawona masomphenya pa choti achite. “Koma Ine ndipita ndikamudzutse iye.” Hum! Ndi zimenezotu pamenepo.

¹⁵⁸ Muwononi Marita akubwera kudzamuwona Iye. Iye anati, “Ambuye, ngati Inu mukadakhala kuno, m’bale wanga sakadamwalira. Koma ngakhale tsopano, chirichonse chimene

Inu mupemphe kwa Mulungu, Mulungu apereka icho kwa Inu.” Mukuona?

159 Iye ankadziwa chimene Iye akanati adzachite. Muwoneni Iye pa manda a Lazaro. Iye anati, “Atate, ine ndikukuthokozani Inu, Inu mwandimva kale Ine, koma Ine ndangonena izo chifukwa cha iwo amene ayima apawa.”

160 “Lazaro, dzuka!” Ndipo Lazaro anaukitsidwa kwa akufa.

161 Tsopano, Iye sananene kalikonse za kufooka pamenepo. Ameneyo anali Mulungu akugwiritsa ntchito mphatso Yake. Ndipo anthu amene ankagwiritsa ntchito mphatso ya Mulungu amakhala osinthika.

162 Pakuti, Iye anali Mawu. “Ndipo Mawu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse,” limatero Baibulo, “ndipo amazindikira zolingirira ndi zamkati mwa mtima.” Zimenezo zimatsimikizira kuti Mulungu ali pakati pa anthu. Inde. Tiyeni tikhulupirire zimenezo. Iye wakonzeka, molingana ndi Mawu Ake, kuti ayitanidwe powonekera, usikuuno.

163 Ndi angati ali muno amene akudwala ndi osowa, kwezani mmwamba manja anu. Tiyeni tiwone manja anu, ndi angati akudwala ndi osowa, kulikonseko. Chabwino, chinthu chokhacho chimene Iye akuchiyembekezera ndicho kuyitanidwa powonekera. Ingomufunsani Iye.

164 Tsopano nanga bwanji ngati Iye akanati wayima pano ndi suti iyi yomwe Iye anandipatsa ine, ndipo inu nkubwera patsogolo pa Iye ndi kudzati, “Ambuye Yesu, ndikufuna kuti Inu mundichiritse ine,” inu mukudziwa chimene Iye akanadzanena? “Ine ndinachita kale zimenezo.”

165 “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi kukhiringwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Iye sangakhoze kuchita izo kachiwiri. Chotero, onani, Iye anachita kale izo. Inu muyenera kukhulupirira zimenezo. Palibe chimene mungachite, kuyenereza kwa chirichonse, kuti—kuti mupeze chipulumutso chanu kapena machiritso. Palibe chirichonse chimene mungachite. Ndi mphatso yaulere ya Mulungu. Mwaona, ndi chisomo, mphatso yaulere. Ngati nditakupatsani madola milioni ndipo inu muwongole tayi yanga; ine sindinakupatseni inu iyo; inu mwachita kuigwirira iyo ntchito. Mukuona? Mphatso ya Mulungu ndi yaulere. Chinthu chokhacho chimene inu muyenera kuchita ndi kukhulupirira izo, kuti Iye anakugulirani inu iyi, inuyo. Iye... Zagulidwa kale. Iye anakuchitirani inu zimenezo. Ndipo palibe munthu pa dziko lapansi... .

166 Ine sindikudziwa zomwe mwakhalapo nazo kuno ku Baton Rouge. Chirichonse chikusuntha dzikoli, zotsanzirana ndi zimenezo. Ife tikudziwa kuti zimenezo zikungoyenera kukhala mwanjira imeneyo basi. Koma pamene munthu abwera nkudzakuuzani inu kuti ali ndi mphamvu zokuchiritsani inu, iye akunama. Mulungu yekha ndi amene angachize. “Ine ndine

Yehova Mulungu wako amene ndimachiza nthenda zako zonse.” Iye sadzagawana ulemelero Wake ndi aliyense. Palibe munthu ali ndi mphamvu zochiritsa.

¹⁶⁷ Koma alipo munthu yemwe ali nazo mphatso, kuti amuwonetsere Mulungu. Abusa anu...[M’bale Branham akutsokomola—Mkonzi]. (Pepani.) Iye akhoza kumutenga Mulungu, mwa mphatso ya—ya...Mphunzitsi, iye akhoza kuwafotokoza Mawu mpaka kufika pakuti inu nkuwawona Iwo. Ngati muli nawo maso oti muwonere nawo, inu mudzaziwona izo. Pali ina, mwinamwake mphatso ina. Koma nthawizonse pamakhala mphatso yomwe imawonetsera Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo, kudzera pamenepo, inu enieni muyenera kuti muzikhulupirira izo.

¹⁶⁸ Wochimwa akhoza kubwera kuno ku guwa ali mnyamata kapena mtsikana, pa usinkhu wa zaka fortini zakubadwa, ndipo iwo nkumakubweretserani inu chakudya chanu kuno, ndipo inu nkumalirira kwa Yehova, mpaka kufika zaka nainte zakubada, inu simudzapulumutsidwa konse. Koma inu muyenera choyamba kuvomereza zimene Iye anakuchitirani inu. Mukuona? Inu muyenera kuvomereza izo, inueni. Ndiye mukavomereza, zikatero Iye ndi Wansembe Wamkulu, mkhalapakati, kudzapanga chitetezero pa kuvomereza kwanuko pa zomwe mwakhulupirira.

¹⁶⁹ Tsopano ndicho chinthu chomwecho ndi mphatso mwanjira iyi. Ndi kuchotsapo malingaliro anu omwe kwa inu, ndipo kenako nkuwona zimene Iye akunena kuti muchite.

¹⁷⁰ Ine ndimawawona anthu akubwera pa nsanja, iwo amalumphaka chokwera—ndi—chotsika ndi kumakuwa, ndi kumati, “Oh, M’bale Branham, ine ndiri nacho chikhulupiriro chonse mdzikoli.” Inu mukutani kuno, ndiye? Mukuona? Ndiko—ndiko kutengeka, ndipo osati chikhulupiriro.

¹⁷¹ Chikhulupiriro chenicheni sichimadziwa kugonja. Zinachitika kale. Izo zinatha kale. Mulungu ananena chomwecho, ndipo izo zimatsirizitsa izo, inu mukuona. “Mulungu ananena chomwecho!” Tsopano ndi chinthu chomwecho, nthawi iliyonse. Pamene inu mukukhulupirira izo kwenikweni, izo zimamukhudza Iye.

¹⁷² Tsopano mkazi wamng’ono uja yemwe anakhudza chovala Chake, iye anati, “Ngati nditangokhudza chovala Chake, ine ndikhala wamphumphu,” ndipo iye anachita zimenezo. Ndipo pamene anachita zomwe chikhulupiriro chake chinafuna kuti achite, “kukhudza izo,” Iye anamverera izo, mwaona, ndipo Iye anapotoloka nalankhula naye.

¹⁷³ Tsopano, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ngati mutangomukhulupirira Khristu, kukhulupirira! Mulole chikhulupiriro chanu chikhudze chovala Chake. Ndipo Iye, pakali pano, ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza

kukhudzidwa ndi zomverera zathu. Ife tonse tikudziwa zimenezo. Ndipo ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Iye ayenera kuchita lero monga Iye anachitira dzulo ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo. Tsopano kodi inu simukukhulupirira zimenezo? Ingokhalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

¹⁷⁴ Ngati ndakuuzani inu bodza, ndiye kuti Mulungu sangaimire kumbuyo zimenezo. Koma ine ndakuuzani inu Choonadi, Iye atero—Iye ayikira kumbuyo Icho. Iye ndi wokakamizika kuchithandizira Choonadi.

¹⁷⁵ Yesu anati, “Ndiri ndi mboni.” Ndipo mboniyo ndi Mawu a Mulungu, ndithudi. Anati, “Pamenepo Malemba akuchitira umboni za Ine. Ngati iwo sakuchitira umboni za Ine, ndiye musawakhulupirire iwo.” Mukuona?

¹⁷⁶ Ndipo ngati Malemba sakuchitira umboni za zimene ine ndikukuuzani inu tsopano, kuti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” ndiye musakhulupirire Lembalo. Chifukwa, Lemba linati Iye anali, ndipo Iye analonjeza zinthu izi kwa m’badwo wotsiriza uno. Kumbukirani, basi pa mathero a m’badwo wa Chiyuda, umo ndi momwe Iye anadziululira Yekha, Mesiya. Mapeto a—m’badwo wa Asamariya, Iye anachita chomwecho. Tsopano ndiko kutha kwa m’badwo wa Amitundu. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

¹⁷⁷ Mudzutseni Iye mu chikumbumtima chanucho, muitanireni Iye powonekera, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

¹⁷⁸ Atate Akumwamba, Mawu okha ochokera kwa Inu tsopano akhala okwanira, Izo zidzakhala zonse zomwe ife tikuzisowa, Mawu okha ochokera kwa Inu. Mulole anthu amvetse bwino zomwe kupindulako, chimene ife tikuyesetsa kuti tichite, Ambuye, ndi kuti—ndi kuwalola kuti alandire madalitso a Ambuye Yesu amene amawakonda ndi kuwatumikira, mulole iwo achite zimenezo usikuuno, Ambuye, chifukwa imfa Yanu siinali pachabe, Inu “munavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, munatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu, chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti aliyense muno, mu Kukhalapo Kwauzimu, amvetse izi ndipo adzapeze masomphenya, ndipo achiritsidwe kwa ulemelero wa Mulungu. Kudzera mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikudzipereka ndekha ndi osonkhana awa, kwa ulemu Wake ndi ulemelero. Amen.

¹⁷⁹ Tsopano mukhale olemkeza kwenikweni, kwa maminiti pang’ono okha. Tsopano Mawu okha ochokera kwa Iye atanthauza zochuluka kuposa zonse zomwe ine ndikanakhoza kunena, kapena wina aliyense akanakhoza kunena, chifukwa ndi Iyeyo akuchita izo. Iye ndi Mmodziyo. Iye ndi Wochita, ndipo

ife tikudalira kuti—Ambuye Yesu apereka zinthu izi kwa inu tsopano, aliyenseyo.

¹⁸⁰ Tsopano tiyeni tiwone nthawi. Sindimadziwa kuti inali chomwecho. Ine ndikukuuzani inu, kuti tituluke pano pa nthawi yake, zomwe tikuyenera kutero, tiribe nthawi yobweretsa mzere uwu. Tiyeni tiyitane iwo kuchokera mwa omvetsera.

¹⁸¹ Tsopano tiyeni tingotenga Lemba, miniti yokha. Tsopano Baibulo limalonjeza, mu tsiku lino, kuti kubwereza kwa Sodomu ndi Gomora kudzabwerezedwa. Ndi angati akukhulupirira zimenezo tsopano, kwezani mmwamba dzanja lanu? Baibulo limadziwitsa zimenezo tsopano.

¹⁸² Ndiyeno chinali chiyani icho ku Sodomu ndi Gomora? Anali Mulungu mu mawonekedwe a munthu. Ndipo momwe Abrahamu anadziwira izo, ndi pamene Iye anati, “Nchifukwa chiyani Sarah anaseka mu hema, kumbuyo? Kapena, nchifukwa chiyani iye anakaikira izo, Mawu amene Iye anali atayankhula kuti anali chomwecho?” Iye amakhoza kuzindikira chimene Sarah anali kuganiza, kumbuyo kwa Iye. Tsopano inu mungowona ngati izo sizinali chomwecho.

¹⁸³ Tsopano, zimenezo sizinali za kwa mpingo waku Babeloni, kapena mpingo wa Sodomu. Ayi, ayi. Izo sizinali kwa anthu amenewo kumusi uko mu maudindo achipembedzo. Ayi, bwana, samapita konse kwa iwo. Iwo anamutenga mtumiki wawo. Mukuona?

¹⁸⁴ Koma kwa Mpingo wosankhidwa, Mbewu yapamwamba ya Abrahamu yomwe ikuyenera kukhulupirira Mawu mosalabadira momwe zinthu ziriri, “Abrahamu anazitcha zinthu zomwe kunalibe ngati kuti zinalipo.” Mulungu ananena chomwecho, ndipo Iye anazikhulupirira izo. Tsopano, mzanga, ine—ine ndikudziwa kuti Mulungu ali wokakamizika kwa Mawu awa, kuti awasunge Iwo.

¹⁸⁵ Tsopano ine ndikufuna inu, kulikonse kumene inu muli mchipinda chino, kuti mukhale molemekeza kwa mphindi pang’ono, kulikonse kumene inu muli. Ndipo mukhulupirire, mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse.

¹⁸⁶ Tsopano ngati ine ndikanakhoza kukuchizani inu, ngati ine ndingakhoze kumuchiza mtsikana wamng’ono uyu yemwe mtima wanga ukumumvera chisoni, ngati ine ndingakhoze kuchiza kanthu kakang’ono kamene kali pamenepo, ine—ine—ine ndikanatero—ine ndikanakwawa kuchokera pano kupita ku North Pole, ngati ine ndingakhoze, kuchita zimenezo, kapena aliyense yemwe ali ndi kumverera kwaumunthu kulikonse. Koma ine sindingathe kuchita zimenezo. Mwina wake ena a inu kumeneko simukhala moyo koma pang’ono pokha, ndi khansa. Ngati ndingakhoze kukuchizani inu, ine ndingakhale. . . Ine sindingakhale woyenera kudzaima pa nsanja iyi ngati ndingathe kuchita zimenezo ndipo osakwanitsa kuchita izo. Tsopano, ine

Mkwatibwi woitanidwa kuchokera pakati pa Amitundu. Ndicho chizindikiro chawo chotsiriza, zonse za zimenezo.

¹⁹⁴ Mulembe zimenezo mu bukhu lanu. Ndine bambo wokalamba. Koma mungolembe zimenezo mu bukhu lanu ndi kudzawona ngati izo zidzafike pochitika, kapena ayi. Mwaona, inu muli kumapeto tsopano. Liti? Ine sindikudziwa. Ine ndikumuyembekezera Iye lero. Ngati Iye sakhala pano lero, ine ndikhala ndikumuyembekezera Iye mawa. Ngati Iye sadzakhhalapo mawa, ine ndidzakhala ndikumuyembekezera tsiku lotsatiralo. Ngati Iye sali pano chaka chino, ine ndidzakhala ndikumuyembekezera Iye chaka chamawa. Ine ndikudziwa Iye akubwera. Ine sindikudziwa miniti kapena ora, koma ine ndikudziwa chirichonse chakwaniritsidwa, kukonzekera Mkwatulo. Mpingo waitanidwa utuluke. Kudzakhala kupita kwa chinsinsi; kungosowa, ndipo izo zidzakhala zonsezo.

¹⁹⁵ Ndipo dziko lizidzapitirirabe chimodzimodzi basi, anthu kumalalikira, ndipo anthu kumaganiza kuti akupulumutsidwa, ndendende basi monga iwo anachitira mu masiku a Nowa, zina zotero. Nowa analowa mu chombo, ndipo anthu ankapitirirabe, ndipo dziko kumazungulira chimodzimodzi basi. Taganizirani za zimenezo! Ndipo, otayika Mwamuyaya, kumaganiza kuti iwo anapulumutsidwa.

¹⁹⁶ Ena a masiku awa ndidzabweretsa hema wamkulu m'dera lino, ndikudzangomuzika iye kuno, kuchitira kuti tidzakhoze kudzakhala ndi misonkhano madzulo, ndi malangizo, kotero inu mudzakhoze kumvetsetsa zinthu izi mwabwinoko. Kudzawasonkhanitsa abale athu onse pamodzi kuti tidzakhale ndi misonkhano.

¹⁹⁷ Tsopano ngati Yesu Khristu akwaniritse lonjezo Lake, ndiye ife tikhala okakamizika kumukhulupirira Iye. Ine ndikufuna inu nonse, aliyense wa inu, mungokhala ndi chikhulupiriro chophweka chonga cha mwana, kuti mumukhulupirire Iye.

¹⁹⁸ Tsopano pamene inu mungokhala ngati mukuyamba ndi mitu yanu yoweramitsidwa, ndi kuyamba kupemphera, kunena kuti, "Ambuye Yesu, tsopano ndikudziwa kuti mwamuna uyu sakundidziwa ine. Ndipo ndine wosowa. Ndipo tikuwuzidwa kuti Ndinu Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi zomverera za zifooko zathu. Ngati Inu mutangomulola iye... Ngati ine ndingakhoze kukukhudzani Inu, ingoyankhulani kudzera mwa iye, Ambuye, kuti nditero, ndikudziwa iye... ndidziwa kuti ndi Inu. Ine ndikudziwa kuti iye sakundidziwa ine."

¹⁹⁹ Ndipo ndizo kunja uko mwa omvetsera, omvetsera osakanikirana basi; okhulupirira, osakhulupirira, odzipangitsa-kukhulupirira; ochimwa, oyera, ndi onse pamodzi.

²⁰⁰ Tsopano inu muyenera kukhulupirira. Tsopano ngati Iye angachite izi kuchokera mwa omvetsera awa pano, ine ndikufuna aliyense wa inu muno, munene kuti, “M’bale Branham, ine—ndikudziwa kuti—ameneyo ayenera kukhala Iye amene akuyang’ana pa osonkhana monga Iye ankachitira nthawi imeneyo.” Ine ndikufuna inu, ngati inu mungakhulupirire kwenikweni, ine ndikufuna inu mukweze dzanja lanu, munene kuti, “Ambuye, ine ndizilandira izo ndi mtima wanga wonse, kuti ine ndikukhulupirira kuti ndi Khristu Yesu, molingana ndi lonjezo Lake.” Ponseponse mchipinda. Mulungu akudalitseni inu. Izo nzabwino. Oh, ndi zosakhala bwino basi kuti tiribe mwezi umodzi wokhala kuno. Mwaona, mungolola. . . Ndine watsopano kwa inu. Mwaona, ndi zovuta. Inu musingokhulupirira.

²⁰¹ Tsopano, ndiko Kuwala. Mulungu ndi Kuwala, ife tikudziwa zimenezo, Lawi la Moto. Ndipo tsopano inu mungopemphera ndi kuchikhudza Icho, ndipo mulole Ambuye Yesu ayankhe.

²⁰² Tsopano ine ndikuwutengera mzimu uliwonse muno pansa pa ulamuliro wanga, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa ulemelero Wake. Tsopano mukhale molemekeza kwenikweni. Pempherani. Khalani olemkeza kwenikweni.

²⁰³ Tsopano, ndi Izi apa. Pali dona pomwe pano patsogolo panga. Iye waweramitsa mutu wake, ndipo iye akupempherera kusautsika kwake komwe. Ngati mukufuna kuti mukweze mutu wanu tsopano, iye ali pomwe pano patsogolo panga. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza matenda a shuga amenewo ndi kukupangani inu kukhala wabwino? Tsopano, ndi zomwe muli nazo, matenda a shuga. Ine sindikukudziwani inu. Ndinu mlendo kwathunthu kwa ine. Koma kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Ngati—ngati ndife alendo kwa wina ndi mzake, kwezani mmwamba dzanja lanu, monga *choncho*, kuti anthu awone. Mukuona? Chabwino. Mwaona, apa pali dona. Ndipo tsopano iye akuvutika ndi matenda a shuga. Ndipo inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Kodi izo zingakupangitseni inu kukhulupirira? Ndinu Akazi a Martin. Ngati izo ziri zoon, kwezani dzanja lanu. Mukuona? Inu mungokhala ndi chikhulupiriro. Musakaikire ayi. Mukhale ndi chikhulupiriro.

²⁰⁴ Tsopano kodi iye anakhudza chiyani? Ine ndikufuna kufunsa omvetsera. Kodi iye anakhudza chiyani? Pali mkazi ali ndi dzanja lake lamanja mmwamba, ndi langa, aponso, pamaso pa Mulungu. Mukuona? Iye anakhudza Chinachake. Mkazi wamng’ono chabe, izo kwenikweni, kuti ndikuuzeni inu choonadi, tsopano inu mukuwona ngati izi ziri zoon, izo zinamudabwitsa iye. Sanadziwe kuti anali ndi chikhulupiriro chochuluka chomwecho. Chikhulupiriro si chinachake chomwe

umachipukusa; ndi chimachake chimene iwe uli nacho. Mukuona? Anadabwitsidwa. Ngakhale pakali pano mkaziyo akumva mosiyana ndi zomwe anachita mphindi zingapo zapitazo. Iye akudziwa kuti chinachake chamuchitikira.

²⁰⁵ Apa, kodi inu simukuwona Kuwala kumeneko? Kulondola. Mwakuwona Iko pomwe apa pa mkazi uyu pomwe apa, kumbuyo komwe kuno? Iye akuvutika ndi a . . . Iye waweramitsa mutu wake pansi. Iye akupemphera. Koma akuvutika ndi nsana wake. Ngati iye ati akhulupirire ndi mtima wake wonse, iye akhoza kuchiritsidwa ku vuto la nsana limenelo. Ndithudi.

²⁰⁶ Iye achiponya icho, motsimikiza monga chirichonse. Mwaona, pemphero lake likupitirirabe. Ambuye, ndithandizeni ine. Akazi a DeVille, ndi inuyo. Chimenecho ndi chisomo. Mkaziyo amapemphera, sanali kuganiza nkomwe, samandimva nkomwe ine ndikunena kalikonse. Tsopano mumufunse iye ngati amandidziwa ine. Ndi yemwe iye ali, ndipo ndiro limene liri vuto lake.

²⁰⁷ Kodi iye wakhudza chiyani? Ndiko kutsimikizira kwa Yesu Khristu, Mawu, amazindikira malingaliro omwe ali mu mtima.

²⁰⁸ Kodi inu mukukhulupirira? Mungokhala ndi chikhulupiriro. Mupemphere konsekonse. Mungokhulupirira. Ndizo zonse zomwe muyenera kuchita. Mungokhulupirira, mungokhulupirira kuti ine ndakuuzani inu Choonadi. Tsopano, ine sindine Iye. Ine ndine wantchito Wake basi, wantchito Wake basi.

²⁰⁹ Ngati mutangokhala ndi chikhulupiriro chokwanira! Ine sindingathe kumuitana iye. Ine ndikudziwa lomwe liri vuto lake, koma, mwaona, mungodikirira kanthawi ndipo mwinamwake izo zisintha. Ndithudi ndi zosatheka, koma muyenera kuchoka mu chotchinga chimenecho. Iye sangadzikhulupirire yekha. Muyenera kumukhulupirira iye.

²¹⁰ Dona akuvutika ndi vuto la impsyo. Iye si wochokera kuno. Akuhokera ku Mississippi. Iye akakhulupirira ndi mtima wake wonse, Mulungu achiza vuto la impsyolo. Akazi a Palmer, ngati inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kuchiritsidwa kwa izo. Izo zakusiyani inu. Kuwala pa iye. Kwachoka pa iye. Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Musati mukaikire.

²¹¹ Pali dona wakhala pafupi ndi iye. Iye akuvutika ndi nyamakazi. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu, dona? Inu mukutero? Kodi mukukhulupirira ngati Mulungu ati andiuze ine yemwe inu muli, kodi izo zikuthandizani inu kuti mukhulupirire? Dzina lanu ndinu Akazi a Meadow. Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse tsopano, inu mukhoza kuchiritsidwa, inunso.

²¹² Izo zinayatsa moto kwa mayi wina yemwe anali pafupi naye. Iye wakhala pamenepo, nayenso. Pamenepo Iko kukupita,

chotsika mzerewo. Dona wakhala pamenepo, akuvutika ndi . . . Pafupi ndi iye, akudwala matenda a shuga, matenda a shuga. Iwo akufuna kuti apite ku chipatala, koma iye akukana kuti achite zimenezo. Iye ali ndi mwana wamwamuna yemwe akumupempherera, aponso. Mwana ameneyo sali kuno, koma kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine chimene chavuta ndi mwana ameneyo? Ali ndi vuto la mtima. Inu mukhulupirire, ndipo Iye akuchizani inu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Akazi a Dufflee, D-u, ma f awiri, l, ma e awiri. Mokhala ngati . . . Ndi choncho. Nkulondola kumeneko, kwezani mmwamba dzanja lanu, ndi manja anu mmwamba. Chabwino. Tsopano inu mukukhulupirira, ndipo inu mukhoza kuchiritsidwa, inunso.


²¹³ Kodi inu mukukhulupirira kuti icho ndi chinthu chomwecho chimene icho . . . Inu mukukhulupirira kuti Kukhalapo kwa Yesu Khristu kuli pano tsopano? Ndi angati mukuvomereza zimenezo? Oh, ndi chitetezo chotani! Ndi chitetezo chotani!

²¹⁴ Mwaona, kodi inu munachita chiyani? Inu munamudzutsa Iye. Inu munamubweretsa Iye powonekera. Apa Iye ali powonekera. Tsopano, sizikupanga kusiyana kulikonse zomwe bwato likunena. Kumbukirani, Iye akhoza kunena kuti, “Mtendere, pakhale bata.”

²¹⁵ Kodi inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse? Ngati mukutero, imirirani pa mapazi anu ndipo muvomereze izo. Imirirani ndipo munene kuti, “Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse.” Muimirire pa mapazi anu. “Ine tsopano ndikukhulupirira.” Ndiko kulondola, ziribe kanthu lomwe liri vuto lanu, muimirire, mpatseni Iye Matamando.

²¹⁶ Atate Akumwamba, tikubweretsa kwa Inu omvetsera awa. Iwo akudziwa kuti Inu muli pano, Ambuye.

Mulole mdierekezi aliyense, kusakhulupirira, zisiye kugwira kwake, ndipo mulole Yesu Khristu akuchizeni nonse inu.

²¹⁷ Satana, tuluka mwa omvetsera awa! Mu Dzina la Yesu Khristu, iwe wakanidwa. 

64-0319 Kumuitanira Yesu Powonekera
Denham Springs High School
Denham Springs, Louisiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org